
# ZIKHULUPIRIRO ZA BAPTIST




TOM SMALL

# ZIKHULUPIRIRO

# ZA BAPTIST

TOM SMALL

**3. Kumwamba kudzakhala ku malo kumene cimo siridzalowako.**

*"Ndipo simudzalowa konse momwemo kanthu kali konse kosapatulika kapena iye wakucita conyansa ndi bodza; koma iwo okha olembedwa m'buku la moyo la Mwanawankhosa."* Cibvumbulutso 21:27

*"Kapena simudziwa kuti osalungama sadzalandira Ufumu wa Mulungu."* 1 Akorinto 6:9a

*"Kwa Iye amene anatikonda ife, natimasula ku macimo athu ndi mwazi wace."* Cibvumbulutso 1:5b

Mkristu amalowa Kumwamba cifukwa Yesu anayeretsa zocimwa zace. Pamene Yesu anafa pa mtanda anatenga zoipa zathu naziika pa Iye yekha. Anatibvekanso cilungumo cace.

**4. Kumwamba ndi malo a cipembedzo.**

*"Ndipo sindinaona kacisi momwemo; pakuti Ambuye Mulungu wamphamvuyonse, ndi Mwanawankhosa ndiwo kacisi wace. Ndipo pa mzindapo sipafunika dzuwa, kapena mwezi wa kuuwalira; pakuti ulemelero wa Mulungu uunikira umenewu, ndipo nyali yace ndiye Mwanawankhosa. Ndipo a mitundu adzayenda-yenda mwa kuunika kwace; ndi mafumu a dziko atenga ulamuliro wao kulowa nao momwemo."* Cibvumbulutso 21:22-24

*kuno kunkakwa inu sangathe, kapena kucokera kwanuko kuyambuka kudza kwa ife, sangathenso."* Luka 16:26

**3. Gahena ndi malo a iwo amene adakana cifundo ca Mulungu mwa Kristu Yesu.**

Mulungu safuna wina aliyense kuti apite ku Gahena. Cifukwa ca cifundo cace ca pa ife, Mulungu anapanga njira ya cipulumutso pa kutumiza Mwana wace kudzafa m'malo mwathu. Ngati munthu akonda njira ya macimo nkana kulapa ndi kukhulupirira Yesu, pamenepo munthuyo ayenera kudzisenzera yekha mphoto ya macimo ace.

*"Wosafuna kuti ena aonongeke, koma kuti onse afike ku kulapa."* 2 Petro 3:9b

*"Koma iye amene sakhulupirira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. Koma ciweruzo ndi ici kuti kuunika kunadza ku dziko lapansi, ndipo anakonda mdima kuposa kuunika, pakuti nchito zao zinali zoipa."* Yohane 3:18b-19

## KUMWAMBA

Buku Lopatulika litiphunzitsa zambiri zadabwitsa za kumwamba motero kuti cidzakhala cosatheka kuganizira zonsezi pamalo ocepawa. Komabe tifuna tiganizire zinthu izi:-

**1. Kumwamba ndi malo a pamaso pa Mulungu ndi Yesu Kristu.**

*"Ndipo Iye ananena naye, Indetu, ndinena ndi iwe, Lero lino udzakhala ndi Ine m'Paradaiso."* Luka 23:43

*"M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ngati sikukadakhala kotero, ndikadakuuzani inu; pakuti ndipita kukukonzerani, inu malo. Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha; kuti kumene kuli Ineko, mukhale inunso."* Yohane 14:2-3

*"Taonani, cihema ca Mulungu ciri mwa anthu, ndipo adzakhalitsa nao; ndi iwo adzakhala anthu ace, ndi Mulungu yekha adzakhala nao, nakhala Mulungu wao."* Cibvumbulutso 21:3b

**2. Kumwamba ndi malo a cimwemwe cosatha.**

*"Ndipo adzawapukutira misozi yonse kuicotsa pa maso pao, ndipo sipadzakhalanso imfa, ndipo sipadzakhalanso maliro; kapena kulira; kapena cowawitsa, pakuti zoyambazo zapita."* Cibvumbulutso 21:4



# ZIKHULUPIRIRO ZA BAPTIST

Published by
Baptist Publishing House
P.O. Box 31995, 10101
Lusaka, Zambia

Printed by
Baptist Printing Ministry
P.O. Box 31995, 10101
Lusaka, Zambia

Copyright, 2011,
International Publications Services
All Rights Reserved
www.ipsimb.com
ipsid: bb-zam-nya

MUTU 14

## CILANGO COSATHA

Pa maphunziro athu oyamba aja tawerenga kuti Buku Lopatulika litiphunzitsa kuti kudzakhala kuuka kwa akufa kwa anthu olungama ndi osalungama. Taphunziranso kuti anthu onse adzaweruzidwa.

Citatha ciweruzo, pali malo okhalamo a muyaya Kumwamba kapena ku gahena. Aliyense adzakhala moyo wa muyaya kumwamba kapena ku gahena. Cifukwa cace tiyeni tione cimene Mau a Mulungu atiphunzitsa za malo awiri amenewa.

## GAHENA

1. **Gahena ndi malo ndithu.**

Pali anthu ena amene amakana kuti kulibe malo ena acilango cosatha amene ali Gahena. Munthu angathenso kukana kuti kulibe dzuwa koma liripo ndithu. Buku Lopatulika litiphunzitsa kuti Gahena ndi malo ndipo Yesu anatifera kuti tipulumuke ku malo amenewa. Werengani bwino pa Luka 16:19-31 musanawerenge zitsanzo izi zalembedwa m'phunzirori.

*"Ndipo mwini cumayo adafanso, naikidwa m'manda; ndipo mu Hade anakweza maso ace, pokhala nao mazunzo."* Luka 16:22b-23a

*"Ndipo amenewa adzacoka kunka ku cilango ca nthawi zonse."* Mateyu 25:46a

*"Komatu amantha, ndi osakhulupirira, ndi onyansa, ndi ambanda, ndi acigololo, ndi olambira mafano, ndi onse amabodza, colandira cao cidzakhala m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure; ndiyo imfa yaciwiri."* Cibvumbulutso 21:8

*"Amene adzamva cilango, ndico cionongeko cosatha cowasiyanitsa ku nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemelero wa mphamvu yace."* 2 Atesalonika 1:9

**2. Gahena ndi malo osathawika.**

Mulungu mwaulere apereka cifundo cace mwa Kristu Yesu kwa onse. Koma pamene munthu akhala wa moyo ndiponso atafa alikukanabe cifundo ca Mulungu, pamenepo palibe ciyembekezo kwa iye. Palibe mwai wina kapena kuthawa ku Gahena.

*"Ndipo pamwamba pa izi, pakati pa ife ndi inu, pakhazikika phompho lalikuru, kotero kuti iwo akufuna kuoloka, kucokera*

*oledzera, kapena olaratira, kapena olanda, sadzalowa Ufumu wa Mulungu."* 1 Akorinto 6:9-10

*"Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'buku la moyo anaponyedwa m'nyanja ya moto."* Cibvumbulutso 20:15

**IWO AMENE ADZAPULUMUTSIDWA PA CIWERUZO**

Palibe munthu adzapulumuka cifukwa ca cilungamo cace, koma cifukwa walapa, nalandira Yesu monga Mpumulutsi, naima pamaso pa Mulungu mwa cilungamo cimene Yesu anampatsa pa kumufera iye.

*"Wokhulupirira Iye saweruzidwa."* Yohane 3:18a

*"Indetu, indetu, ndinena kwa inu, kuti iye wakumva mau anga, ndikukhulupirira Iye amene ananditumа Ine, ali nao moyo wosatha, ndipo salowa m'kuweruza, koma wacokera ku imfa, nalowa m'moyo."* Yohane 5:24

*"Ameneyo sanadziwa ucimo anamyesera ucimo m'malo mwathu, kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa Iye."* 2 Akorinto 5:21



**ZIKHULUPIRIRO ZA BAPTIST**


1. Buku Lopatulika ........ 5
2. Mulungu ........ 11
3. Ambuye Yesu Kristu ........ 18
4. Mzimu Woyera ........ 22
5. Cimo ndi Satana ........ 28
6. Cipulumutso ........ 33
7. Mpingo wa Mulungu ........ 37
8. Malamulo a Mpingo ........ 43
9. Kukhala Woyang'anira ........ 49
10. Tsiku Lopembedza ........ 53
11. Kubweranso kwa Ambuye ........ 56
12. Kuuka kwa Akufa ........ 59
13. Ciweruzo ........ 62
14. Moyo Wosatha, Cilango Cosatha ........ 64

## BUKU LOPATULIKA

Pali mafunso ena amene amafunsidwa kawiri-kawiri onena za Buku Lopatulika. Pa phunziro ili tidzaganizira za mafunso amenewa mosamala kuti tione ngati tingathe kupeza mayankho ace.

## KODI BUKU LOPATULIKA NCIANI?

Buku Lopatulika liri lopangidwa ndi mabuku ang'ono-ang'ono ndipo ambiri-mbiri amene anaikidwa pamodzi kupanga cibuku cacikuru. Tikayamba kuyang'ana m'Buku Lopatulika lathu, timaona kuti liri logawidwa magawo osiyana-siyana. Gawo liri lonse liri ndi dzina lace monga kunena kuti Genesis, Eksodo, Mateyu ndi ena otere. Kale-kale gawo liri lonse la mabuku awa makumi asanu ndi limodzi kudza mphambu zisanu ndi imodzi (66) linali kabuku kakang'ono pa kokha. Tsopano mabuku onse amenewa anaundidwa pamodzi kupanga cibuku cacikuru cimodzi cochedwa Buku Lopatulika.

Buku Lopatulika liri ndi magawo akuru-akuru awiri. Gawo loyamba liri lopangidwa ndi mabuku makumi atatu kudza mphambu zisanu ndi zinai (39) a Buku Lopatulika; ndipo gawo limeneli lichedwa Cipangano Cakale. Gawo laciwiri liri lopangidwa ndi mabuku makumi awiri kudza mphambu zisanu ndi ziwiri (27) amene ali kotsilizira kwace kwa Buku Lopatulika, ndipo gawo limeneli lichedwa Cipangano Catsopano. Gawo ili linalembedwa utatha utumiki wa pansi pano wa Ambuye Yesu.

Buku Lopatulika ndi buku la kale-kale. Genesis, buku loyamba la m'Buku Lopatulika, linalembedwa pa zaka mazana khumi ndi anai (1400) Ambuye Yesu asanabadwa. Cibvumbulutso, buku lotsiliza la Buku Lopatulika, linalembedwa patapita zaka zana limodzi (100) Ambuye Yesu atabadwa. Taonani tsopano kuti mabuku onse awa (66) analembedwa mu nthawi yokwanira zaka mazana khumi ndi asanu (1500) Buku la kumapeto kwace kwa Buku Lopatulika linalembedwa pa zaka zikwi ziwiri (2000) zapitazi. Indedi, Buku Lopatulika ndi la kale-kale, koma timaona kuti uthenga wace uli woona lero lino monga momwe unali pa nthawi yolembedwa. Udzakhalabe uthenga woona pa zaka zonse za mtsogolo.





## COONADI CA CIWERUZO CIMENE CIRINKUDZA

Mau a Mulungu atiuza ife kuti zoonadi tsiku lirikubwera limene Mulungu adzaweruza anthu onse.

*"Ndipo popeza kwaikikatu ka anthu kufa kamodzi, ndipo atafa, ciweruziro."* Ahebri 9:27

*"Cifukwa anapangira tsiku limene adzaweruza dziko lokhalamo anthu m'cilungamo, ndi munthu amene anamuikiratu; napatsa anthu onse citsimikizo, pamene anamuukitsa kwa akufa."* Macitidwe 17:31

*"Tsiku limene Mulungu adzaweruza ndi Yesu Kristu zinsinsi za anthu, monga mwa uthenga wanga wabwino."* Aroma 2:16

## IWO AMENE ADZAFIKA KU CIWERUZO

*"Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wa kuweruza wa Kristu, kuti yense alandire cocitika m'thupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa."* 2 Akorinto 5:10

*"Ndipo adzasonkhanidwa pa maso pace anthu a mitundu yonse, ndipo iye adzalekanitsa iwo wina ndi mnzace, monga mbusa alekanitsa nkhosa ndi mbuzi."* Mateyu 25:32

*"Ndipo ndinaona akufa, akuru ndi ang'ono alimkuima pamaso pa Mulungu."* Cibvumbulutso 20:12a

## IWO AMENE ADZAKANIDWA PA CIWERUZO

Munthu amakanidwa ndi Mulungu cifukwa ca cimo. Akhalabe okanidwa cifukwa ca kukana Yesu kwace kuti simpulumutsi ndi Mbuye wace. Pamene munthu akana cikondi ca Mulungu ndi cifundo ca mwa Kristu, palibe thandizo kwa iye. Iwo amene akufa pamene alikukanabe Yesu monga Mpulumutsi wao adzakanidwa pa ciweruzo.

*"Wosakhulupirira waweruzidwa ngakhale tsopano, cifukwa sanakhulupirira dzina la Mwana wobadwa yekha wa Mulungu. Koma ciweruzo ndi ici, kuti kuunika kunadza kudziko lapansi, ndipo anthu anakonda mdima kuposa kuunika; pakuti nchito zao zinali zoipa."* Yohane 3:18b-19

*"Kapena simudziwa kuti osalungama sadzalandira ufumu wa Mulungu? Musasoceretsedwe, adama, kapena opembedza mafano, kapena acigololo, kapena olobodoka ndi ziopa, kapena akudziipsa ndi amuna; kapena ambala, kapena osirira, kapena*

*"Ndi kukhala naco ciyembekezo ca kwa Mulungu cimene iwo okhanso acilandira, kuti kudzakhala kuuka kwa olungama ndi osalungama."* Macitidwe 24:15

## ZOTSATIRA ZACE ZA KUUKA KWA AKUFA KUKUBWERATU PA MIYOYO YATHU

Citsimikizo cokondweretsa ndico cakuti pamene timwalira tidzakhala ndi Ambuye Yesu Kristu kwa muyaya.

*"Pakuti tidziwa kuti ngati nyumba ya pansi pano ya msasa wathu upusuka, tiri naco cimango ca kwa Mulungu, ndiyo nyumba yosamangidwa ndi manja, yosatha, m'Mwamba."* 2 Akorinto 5:1

*"Komatu tirimbika mtima, ndipo tikondwera maka-maka kusakhala m'thupi, ndi kukhala kwathu kwa Ambuye."* 2 Akorinto 5:8

2. Kudziwa za kuukanso kwa akufa kumene kudzadza kutipanga ife kutipanga ife kuti tidzipereke pakucita nchito ya Ambuye molimbika.

*"Cifukwa cace, abale anga okondedwa, khalani okhazikika, osasunthika, akucuruka mu nchito ya Ambuye, nthawi zonse, podziwa kuti kucititsa kwanu sikuli cabe mwa Ambuye."* 1 Akorinto 15:58



## ANALEMBA BUKU LOPATULIKA NDANI?

Ili ndilo funso limene limasokoneza maganizo a anthu ena cifukwa anamva kuti anthu monga Mose, Yesaya, Paulo ndi anthu ena ndiwo analemba mabuku a m'Buku Lopatulika. Ena amanena kuti Buku Lopatulika ndilo Mau a Mulungu ndipo Mulungu analilemba yekha. Ena anakhala odabwa kuti kungatheke bwanji kuti Buku Lopatulika likhale Mau a Mulungu pamene linalembedwa ndi anthu.

Kapena kufotokoza kumene tiri kuyesa kunena m'ndime za patsogolozi kudzatithandiza kudzindikira m'mene anthu analembela Buku Lopatulika koma ndilo Mau a Mulungu. Tiyeni tione citsanzo ici kuti kapena mfumu yanu inafuna kulemba kalata kwa inu. Mfumuyo inaitana mlembi wace ndi kumuuza mlembiyo zonse zimene ziyenera kulembedwa pa kalatapo. Mlembiyo mokhulupirika analemba zonse bwino-bwino. Inu mutalandira kalatayo mudzanena kuti, "Ine ndalandira kalata yocokera kwa mfumu yanga." Ndipo mau amenewa mudakanena zoonadi. Ngakhale kuti kalatayo inalembedwa ndi munthu wina koma uthenga uli m'menemo unali wocokera kwa mfumu yanu. Ndi cimodzi-modzi ndi Buku Lopatulika. Mulungu, kudzera mwa Mzimu wace Woyera, anaphunzitsa anthuwo cimene akadayenera kulemba ndipo mokhulupirika anazilemba anthuwo. Cifukwa cace, pamene tinena za Buku Lopatulika, timanena kuti ndilo Mau a Mulungu ngakhale kuti tidziwa kuti dzanja la munthu ndilo linalemba mauwa. Monga kalata ija inali uthenga wa mfumu wobwera kwa inu, momwemonso Buku Lopatulika ndilo uthenga wa Mulungu wa kwa yense wa ife.

## TINGATHE KUKHULUPIRIRA BWANJI KUTI BUKU LOPATULIKA LINENA ZOONADI?

Pali zifukwa zambiri zimene tingathe kukhulupirira nazo kuti Buku Lopatulika linena zoonadi. Tiyeni tiganizire zifukwa zitatu izi:

**1. Tikhulupirira kuti Buku Lopatulika liri loonadi cifukwa ca umodzi wace.**

Titanthauza ciani pamene tinena za umodzi wace wa Buku Lopatulika? Tiyeni tiganizire mwa njira iyi. Tiyeni tiyese kunena kuti tasankha kapena anthu makhumi anai (40) ndi kuwapatsa mapepala makumi asanu ndi limodzi kudza mphambu zisanu ndi imodzi (66). Ena akanalandira pepala limodzi ena akanalandira

ambiri. Tiyeni tiganizire kuti anthu amenewa auzidwa kulemba nkhani ina yace pa pepala limene walandira munthu m'modzi aliyense wa iwowa. Ndipo anatumizidwa ku malo osiyana-siyana kuti asalankhulane wina ndi mnzace. Palibe amene anadziwa cimene adzalemba mnzace. Potsiliza talandira mapepala ao onse aja. Kodi pamenepo sicikanankhala cacilendo poona kuti nkhani zolemba aliyense kutali ndi mnzace poziika pamodzi anena cinthu cimodzi-modzi ca nkhaniyo? Tidakanena kuti cotereci sicingacitike pokha-pokha munthu wina atakhala kuti anawauza onsewo mau oyenera kulemba.

Tsopano ganizirani za Buku Lopatulika. Mabuku onse makumi asanu ndi limodzi kudza mphambu zisanu ndi imodzi (66) analembedwa pafupi-fupi kupyola pa nthawi ya zaka mazana khumi ndi asanu (1500) ndipo analembedwa ndi anthu okwanira pafupi-fupi makumi anai (40) osiyana-siyana. Koma pamene mabuku onsewa (66) aikidwa pamodzi alikunena nkhani imodzi ya Mulungu, cikondi cace, ndi njira yace ya cipulumutso kudzera mwa Yesu Kristu. Poona kuti Buku Lopatulika linalembedwa pa nthawi yaitali yotere ndi anthu osiyana-siyana, tidziwa kuti anali Mulungu amene anauza aliyense wa amenewa cimene akanayenera kulemba. Cifukwa Mulungu ndiye anawaphunzitsa zinthu zoti alembe, gawo liri lonse lifanana ndi magawo ena onse kupanga mbiri yonse ya Mulungu. Angakhale kuti Buku Lopatulika liri ndi mabuku ambiri-mbiri osiyana-siyana, koma ndilo buku limodzi ndipo liri ndi mlembi weni-weni m'modzi.... Mulungu mwini wace. Ici ndico cimene titanthauza pakunena kuti umodzi wa Buku Lopatulika. Cifukwa kuti Buku Lopatulika liri ndi umodzi umenewu litipangitsa ife kuti tikhulupilire kuti Buku Lopatulika linena zoonadi.

**2. Tikhulupirira kuti Buku Lopatulika linena zoonadi cifukwa limalankhula ku mitima yathu.**

Ngati munthu wina anena kuti kuli kudza mvula ndipo ife tiri kuimva pathupi pathu ndi kuiona mvulayo, tidziwa kuti munthuyo alikunena zoona. Molingana ndi kuti manja athu ndi maso athu ziri kutsimikiza kuti kuli mvuladi, Mulungu analenga mitima yathu kuti iyoyo ingathe kudziwa coonadi ca Mulungu ngati titafunadi kuti tidziwe. Yesu anatiuza kuti munthu amene afuna kudziwa za Mulungu ndi muthu amene ali wokonzekera kucita cifuniro ca Mulungu monga momwe caululidwira kwa iye.



*"Kutsala kanthawi, ndipo dziko lapansi silindionanso Ine; popeza Ine ndiri ndi moyo inunso mudzakhala ndi moyo."* Yohane 14:19

*"Usaope, Ine ndine woyamba ndi wotsiriza; ndi wa muyaya, ndipo ndinali wakufa, ndipo taonani, ndiri wa moyo kufikira nthawi za nthawi, ndipo ndiri nazo zofungulira za imfa ndi Hade."* Cibvumbulutso 1:17b, 18

**MAKHALIDWE AKUUKA KWA AKUFA KWA YESU**

Pali zambiri zimene sitidziwa za thupi la Ambuye litaukitsidwa kwa akufa. Komabe, tifuna kuti tiganizire bwino za zinthu zimene tiuzidwa m'Buku Lopatulika kunena za thupi lace louka kwa akufa.

Linali thupilo limene linaikidwa m'manda ndi kuukitsidwa.

*"Palibe kuno Iye, komatu anauka."* Luka 24:6a

Thupi loukitsidwalo linali thupi leni-leni.

*"Penyani manja anga ndi mapazi anga, kuti Ine ndine mwini: ndikhudzeni; ndipo penyani; pakuti mzimu ulibe mnofu ndi mafupa, monga muona ndiri nazo Ine."* Luka 24:39

Thupi loukitsidwalo linali losiyana ndi matupi athu a dziko lino lapansi.

*"Ndipo maso ao anatseguka, ndipo anamzindikira Iye, ndipo anawakanganukira Iye, nawacokera."* Luka 24:31

Thupi loukitsidwalo linatengedwa kunka Kumwamba.

*"Ndipo m'mene ananena izi, ali cipenyerere iwo, ananyamulidwa ndipo mtambo unamlandira Iye kumcotsa ku maso kwao."* Macitidwe 1:9

**KUUKA KWA ANTHU ONSE**

Kudzakhala kuuka kwa akufa kwa onse oipa ndi abwino. Anthu ena amaphunzitsa kuti kulibe moyo wina munthu akafa. Mulungu, m'mau ace, atiphunzitsa ife zosiyana ndi zimenezi.

*"Ndipo ambiri a iwo ogona m'pfumbi lapansi adzauka, ena kunka ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi ndi mnyozo wosatha."* Danieli 12:2

*"Musazizwe ndi ici, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ace; nadzaturukira, amene adacita zabwino, kukuuka kwa moyo; koma amene adacita zoipa kukuuka kwa kuweruza."* Yohane 5:28, 29

## KUUKA KWA AKUFA
## KUUKA KWA AKUPA KWA YESU

Tingathe kudziwa za kuuka kwa akufa kwa Mkristu pakuphunzira bwino za kuuka kwa akufa kwa Yesu, *"Koma tsopano Kristu waukitsidwa kwa akufa, cipatso coundukura ca iwo akugona."* 1 Akorinto 15:20. Pamene cimanga ciyamba kuca m'munda, cimanga cimodzi ndico cidzayamba kuca. Ndico cipatso coyamba. Conse cimene cidzaca pambuyo pace cidzakhala ngati icoci. Kusiyana kuli pa nthawi pokha....osati mtundu. Ndi cimodzi-modzi ndi Kristu, cipatso coyamba ca kuuka kwa akufa. Kuuka kwa akufa kwa Akristu kudzakhala kotsatira ndipo adzakhala monga Iye.

**1. Coonadi ca kuuka kwa Yesu.**

Palibe cofunsa pa coonadi cakuti Yesu anafadi pa mtanda. Anapacikidwa pa mtanda poonekera kwa anthu onse ndipo uyinji wa anthu ambiri unasonkhana kuonerera. Adani ace anatsimikizadi kuti anafa. Asilikali amene anaphunzitsidwa za kupha anthu anaona kuti anali wakufadi. Mkondo unapitsidwa m'mbali mwa thupi lace kuonetsetsa kuti wafadi. Pamene mwazi ndi madzi zinaturuka, cinali cidzindikiro cakuti anafadi. Okondedwa ace a Yesu sakanamuika m'manda pakanakhala cidzindikiro coonetsa kuti anali ndi moyo. Imfa ya Yesu inali ya poyera kuti onse aone ndipo sicinali cokaikitsa kuti Yesu anafadi. Kuuka kwa akufa kwace kunali koonadi. Tiyeni tiganizire Mau a Mulungu ena amene aphunzitsa za kuuka kwa akufa kwace.

*"Kwa iwonso anadzionetsera yekha wa moyo ndi zitsimikizo zambiri, naonekera kwa iwo masiku makumi anai, ndi kunena zinthu za Ufumu wa Mulungu."* Macitidwe 1:3

*"Ndi kuti anaonekera kwa Kefa, pamenepo kwa khumi ndi awiriwo; pomwepo anaonekera pa nthawi imodzi kwa abale oposa mazana asanu, amene ocuruka a iwo akhala kufikira tsopano, koma ena agona; pomwepo anaonekera kwa Yakobo, pamenepo kwa atumwi onse; ndipo potsiriza pace pa onse, anaonekera inenso monga mtayo."* 1 Akorinto 15:5-8

Ciyembekezo cathu ca kuuka kwa akufa citsimikizidwa pa coonadi ca kuuka kwa akufa kwa Yesu ndi lonjezo lace.



Mulungu adatithandiza kuti tidziwe za iye ngati tifuna moonadi kucita cifuniro ca Mulungu.

*"Ngati munthu aliyense afuna kucita cifuniro cace, adzazindikira za ciphunzitsoco, ngati cicokera kwa Mulungu, kapena ndilankhula zocokera kwa ine ndekha."* Yohane 7:17.

**3. Tikhulupirira kuti Buku Lopatulika ndi loonadi cifukwa latsimikiza lokha kuti liri loonadi.**

Tiyeni tione njira ziwiri zimene Buku Lopatulika lidzionetsera lokha kuti liri loonadi. Poyamba-yamba lidzitsimikizira lokha cifukwa ca kuneneratu zoonadi za mtsogolo zimene ziri zoonekadi. Ngati wina abwera kwa ife natiuza kuti zinthu zakuti-zakuti zidzacitika patsogolo. Ngati zinthuzi zitacitikadi monga momwe ananeneramo tikuti ananena zoonadi. m'Buku Lopatulika lonse tipeza uneneri wonena za mtsogolo. Pamene tiphunzira za mbiri ya dziko ndi Buku Lopatulika tiona kuti zinthu zimene zinanenedweratu m'Buku Lopatulika zicitikadi monga momwe linalonjezera Buku Lopatulika. Mbiri za dziko zatsimikiza kuti Buku Lopatulika linena zoonadi.

Caciwiri, Buku Lopatulika lidzitsimikizira lokha kuti linena zoonadi pamene tilawa coonadi cace. Tiyeni tiganizire za cimeneci m'njira iyi...kapena muli ndi galimoto. Tsiku lina galimotolo linafa pa mseu. Inu simunali kudziwa kukonza kwace. Tsopano munthu wina anabwera kwa inu ndipo anakuuzani cinthu coti mucite kuti mukonze galimotolo. Pamene munacita monga ananeneramo, galimotolo linayendanso bwino-bwino. Tsopano mukanadziwa kuti munthu uja ananena zoonadi cifukwa galimoto lokonzedwalo ladzicitira umboni lokha kuti ananena munthuyo zinali zoonadi. Ndi cimodzi-modzi ndi Buku Lopatulika. Miyoyo yathu inaonongeka ndi macimo. Pamene tiwerenga, kukhulupirirani ndi kumvera ziphunzitso za Mau a Mulungu, tipeza kuti tiri bwino m'mitima yathu. Pamenepo tidziwa kuti Buku Lopatulika liri loonadi cifukwa lidzionetsera lokha kuti liri loonadi ku miyoyo yathu.

## KODI MULUNGU ANAPEREKA KWA YANI BUKU LOPATULIKA?

Mulungu anapereka Buku Lopatulika kwa anthu onse. Buku Lopatulika sibuku la dziko limodzi kapena la mtundu umodzi wa anthu ai. Buku la Cipangano ca Kale poyamba linalembedwa m'Cihebri, Buku la Cipangano ca Tsopano poyamba linalembedwa m'Cihelene (ci-Griki). Pambuyo pace zonsczi

zinatanthauzidwa m'zinenero za ci-Latini, Cizungu, ci-Jeremani, Cinyanja ndi Cibemba.

Cinali cikonzedwe ca Yesu kuti Uthenga Wabwino ukhale wa anthu onse. Asanakwere kunka kumwamba anauzitsa bwino-bwino akuphunzira ace za cimeneci. Anawauza kuti, *"Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu amitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera: ndi kuwaphunzitsa, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu; ndipo onani, Ine ndiri pamodzi ndi inu masiku onse, kufikira cimaliziro ca pansi pano."*

## CIFUKWA CIANI MULUNGU ANATIPATSA BUKU LOPATULIKA?

Pali zifukwa zikuru-zikuru ziwiri zimene Mulungu anatipatsira Buku Lopatulika. Tiyeni tiganizire zifukwa ziwirizi mwa cidule:

**1. Mulungu anatipatsa Buku Lopatulika kuti munthu wosapulumuka adziwe njira ya cipulumutso napulumuke.**

Pamene Paulo analemba kwa Timoteo, ananena za Mau a Mulungu opatulika; ananena kuti, "...*Okhoza kukupatsa nzeru kufikira cipulumutso, mwa cikhulupiriro cambiri, ndi mbiri idza mwa Mau a Kristu."* Aroma 10:17

Nthawi zonse tizikumbukira kuti ndi Yesu amene amapulumutsa. Ndi nchito yace ya Buku Lopatulika kutiphunzitsa ife za Yesu ndi m'mene tingapulumutsidwere kudzera mwa cikhulupiriro ca mwa Iye.

2. Mulungu anapereka Buku Lopatulika kuti wopulumutsidwawo adziwe kukhala ndi moyo wa Cikristu

*"Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pa ciphunzitso, citsutsano, cikonzero, cilangizo ca m'cilungamo: kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kucita nchito ili yonse yabwino"* 2 Timoteo 3:16-17.

*"Malangizo anu andizindikiritsa; cifukwa cace ndidana nao mayendedwe onse a cinyengo."* Masalmo 119:104.

Poganizira za mau amenewa, tiona m'mene Buku Lopatulika likhudzira mbali zonse za moyo wathu kukhala cocinjiriza cathu pa moyo wa uzimu. Litionetsa ife njira ya cipulumutso ndi kutiphunzitsa ife mmene tiyenera kukhalira monga Akristu.



*ndi kutentha kwa kukuru, ndipo dziko ndi nchito ziri momwemo zidzatenthedwa. Popeza izi zonse zidzakanganuka kotero, muyenera inu kukhala anthu otani nanga, m'mayendedwe opatulika ndi m'cipembedzo; akuyembekezera ndi kufulumira kwa kudza kwace kwa tsiku la Ambuye."* 2 Petro 3:10-12a

*"Okondedwa, tsopano tiri ana a Mulungu, ndipo sicinaoneke cimene tidzakhala. Tidziwa kuti, pakuoneka Iye, tidzakhala ofanana ndi Iye, pakuti tidzamuona Iye monga ali. Ndipo yense wakukhala naco ciyembekezo ici pa Iye, adziyeretsa yekha, monga Iyeyu ali Woyera."* 1 Yohane 3:2, 3

*nkhope ya Ambuye, ndi ku ulemerelo wa mphamvu yace."* 2 Atesalonika 1:7-9

*"Koma miyambo ndi dziko lapansi pano, zaikika ku moto, zosungika kufikira tsiku la ciweruzo ndi cionongeko ca anthu osapembedza."* 2 Petro 3:7

*"Musazizwe ndi ici, kuti ikudza nthawi, imene onse amene ali m'manda adzamva mau ace, nadzaturuka, amene anacita zabwino, ku kuuka kwa moyo, koma amene adacita zoipa ku kuuka kwa kuweruza."* Yohane 5:28, 29

**2. M'mene kubweranso kwa yesu kudzatanthauza kwa opulumutsidwa.**

*"Musazizwe ndi ici, kuti ikudza nthawi, imene onse ali m'manda adzamva mau ace, nadzatulukira, amene adacita zabwino, ku kuuka kwa moyo."* Yohane 5:28, 29a

*"Ndipo ngati ndipita kukakonzera inu malo, ndidzabweranso, ndipo ndidzalandira inu kwa Ine ndekha, kuti kumene kuli Ine ndekha, kuti kumene kuli Ineko, mukhale inunso."* Yohane 14:3

*"Pakuti ambuye adzatsika M'mwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka: pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse."* 1 Atesolonika 4:16, 17

## KUKONZEKERA ZA KUBWERA KWACE

**1. Kukonzekera kwa anthu osapulumutsidwa.**

Pali cinthu cimodzi cokha cimene munthu wosapulumuka angathe kucita kuti akonzekere kubweranso kwa Ambuye. Ayenera kulapa macimo ndi kulandira Yesu Kristu kukhala Mpulumutsi ndi Mbuye wace. (Onani mutu uja wa Cipulumutso).

**2. Kukonzekera kwa anthu opulumuka.**

Munthu wopulumuka ayenera kukhala motsatana ndi cifuniro ca Mulungu tsiku ndi tsiku kuti pamene Yesu abweranso adzamupeza munthuyo ali wokozeka.

*"Cifukwa cace dikirani, pakuti simudziwa tsiku lace lakufika Ambuye wanu."* Mateyu 24:42

*"Koma tsiku la Ambuye lidzadza ngati mbala, m'mene miyambo idzapita ndi cibumo cacikuru, ndi za m'mwamba zidzakanganuka*



## KODI TIMVERE ZIPHUNZITSO ZIMENE ZICOTSAPO KAPENA KUONJEZAPO MAU PA BUKU LOPATULIKA?

Pali zifukwa zitatu zokwanira bwino zimene zitionetsa kuti sitiyenera kumvera ku ziphunzitso zoterezi. Pamene tiri kuganizira za zifukwa izi, tidzaona kuti Mulungu afuna kuti ife titsogozedwe ndi mau ace okha.

**1. Sitiyenera kumvera ziphunzitso zoterezi cifukwa Mulungu anadzionetseratu yekha mwa Kristu Yesu. Cifukwa cace sipangathekenso kukhala ciphunzitso cina coposa ici conena za Mulungu.**

Yesu anati, *"Iye amene wandiona Ine waona Atate; unena iwe bwanji, Mutionetsere Atate? Sukhulupirira kodi kuti ndiri Ine mwa Atate, ndi Atate ali mwa Ine? Mau amene ndinena Ine kwa inu sindilankhula kwa Ine ndekha; koma Atate wokhala mwa Ine acita nchito zace."* Yohane 14:9b, 10.

**2. Tisamvere ziphunzitso zoterezi cifukwa Mau a Mulungu ali oona lero monga momwe anali pa nthawi yolembedwa. Adzakhala mau oona zaka zonse za mtsogolo monga momwe aliri lere. Ndipo mauwa ali okwanira.**

*"Udzu unyala, duwa lifota, koma mau a Mulungu wathu adzakhala nthawi zacikhalire"* Yesaya 40:8.

*"Thambo ndi dziko lapansi zidzacoka, koma mau anga sadzacoka"* Mateyu 24:35.

**3. Tisamvere ziphunzitso zoterezi cifukwa Mau a Mulungu atiuza ife m'buku lotsiliza la m'Buku Lopatulika kuti tisaonjezepo kapena kucotsapo pa mau ace.**

*"Ngati munthu wina aonjezapo pa zinthu izi, Mulungu adzamuonjezera miliri yolembedwa m'bukumu: ndipo ngati aliyense akacotsapo pa mau a m'buku la cinenero ici, Mulungu adzam'cotsera gawo lace m'buku la moyo, ndi munzinda Woyerawo, ndi pa izi zilembedwa m'bukumu."* Cibvumbulutso 22:18, 19.

Mwa ulemu tiyamike Mulungu cifukwa ca kutipatsa mau ace, ndilo Buku Lopatulika. Kudzera mwa ilori tidzadziwa njira ya cipulumutso ndi makhalidwe okondweretsa Mulungu. Tiyeni tiriwelenge, tirikhulupirire, ndipo tirimvere.

## MULUNGU ALIPO

Pamene tiphunzira za Mulungu, tiyeni poyamba tiganizire zakuti Mulungu alipo. Sipafunika kucita kuwerenga Buku Lopatulika kuti tidziwe kuti Mulungu alipodi. Mtima wathu utiuza ife kuti Mulungu alipo. Pali anthu ena pa dziko lapansi amene asanaone Buku Lopatulika, koma amadziwa kuti kuli Mulungu wa mkuru amene analenga kumwamba ndi dziko lapansi. Tiyeni tiganizire zifukwa zina zimene mtima wathu umadziwira kuti kuli Mulungu.

**1. Cilengedwe citiphunzitsa ife kuti kuli Mlengi.**

Pamene tiona cinyumba cacikuru, timadziwa kuti sicinabwere cokha pamenepo mwa ngozi, ai. Ganizirani zinthu zonse zopezeka m'cinyumba cacikuru cimeneci; maziko, zikwi ndi zikwi za njerwa zoikidwa mosamalira bwino, mphuthu za citsulo za mazenela, denga (tsindwi), zipinda ndi makomo ace, zingwe zoyatsira moto, zitseko, kupaka mcenga ndi kupaka njeleza. Tidziwa kuti cinyumbaci alipo amene anacimanga.

Monga momwe cinyumbaci citionetsera kuti alipo amene anacimanga, momwemonso cilengedwe citidziwitsa ife kuti kuli Mlengi amene anazilenga zonsezi. Pamene tiganizira za cilengedwe ndi zodabwitsa zace zonse, timadziwa mumtima mwathu kuti kumwamba ndi dziko lapansi sizinabwere zokha mwa ngozi, ai. Wina wace anazilenga zimenezi. Winayo ndiye Mulungu.

*"Za kumwamba zimalalikila ulemelero wa Mulungu; ndipo thambo lionetsa nchito ya manja ace."* Masalmo 1:20

*"Pakuti, cilengedwere dziko lapansi zaoneka bwino zosaoneka zace ndizo mphamvu yace yosatha ndi Umulungu wace; popeza zazindikirika ndi zinthu zolengedwa, kuti iwo adzakhale opanda mau akuwilingura."* Aroma 1:20

**2. Njara ya munthu yofunafuna Mulungu itiphunzitsa ife kuti kuli Mulungu.**

Ife tiri kukhala pa dziko lapansi pamene pali mayankho onse oyankha njara ya munthu. Mimba ya munthu imamva njara kufuna cakudya, ndipo cakudya cilipo cokhutitsa njarayo. Ku khosi kwa munthu kumamva ludzu lofuna madzi, ndipo madzi alipo akupha ludzulo, ndipo kuwala kulipo. Inde thupi la munthu





## KUBWERANSO KWA AMBUYE

Cimodzi ca zoyambekezera zazikuru za Mkristu ndico kubweranso kwace kwa Ambuye Yesu Kristu. Buku Lopatulika mwina silingathe kutiuza zonse zimene tikanayenera kudziwa za kubweranso kwace, koma pali zisonyezo zina zonena za kubweranso kwace zimene tiyenera kuzidzindikira bwino.

### COONADI CA KUBWERANSO KWACE

*"Pakuti monga mphezi idzera ku m'mawa, nionekera kufikira ku madzulo; kotero kudzakhalanso kufika kwace kwa Mwana wa munthu."* Mateyu 24:27

*"Amenenso anati, Amuna a ku Galileya, muimilanji kuyang'ana kumwamba? Yesu amene, walandilidwa kunka kumwamba kucokera kwa inu, adzadza momwemo monga munamuona alinkupita kumwamba."* Macitidwe 1:11

*"Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpufu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndilipenga la Mulungu."* 1 Ateselonika 4:16a

### KUSADZIWIKA KWA NTHAWI YACE

*"Koma za tsiku ilo ndi nthawi yace sadziwa munthu aliyense, angakhale angelo a Kumwamba, koma Atate yekha."* Mateyu 24:36

*"Cifukwa cace dikirani, pakuti simudziwa tsiku lace lakufika Ambuye wanu."* Mateyu 24:42

*"Koma za nthawi ndi nyengo, abale, sipafunika kuti ine ndikulembereni inu. Pakuti inu nokha mudziwa bwino tsiku ilo Ambuye adzadza monga mbala pakati pa usiku."* (1 Atesalonika 5:1-2)

### ZOCITIKA PA KUBWERANSO KWACE

**1. M'mene kubwera kwa yesu kudzatanthauza kwa osapulumuka.**

*"...Pamene Ambuye Yesu adzabvumbulutsidwa wocokera Kumwamba pamodzi ndi angelo a mphamvu yace, m'lawi la moto, ndi kubwezera cilango kwa iwo osamdziwa Mulungu, ndi iwo osamvera uthenga Wabwino wa Ambuye wathu Yesu Kristu: amene adzamva zilango, ndico cionongeko cosatha cowasiyanitsa ku*

likhalenso tsiku logwira nchito. Komabe, ncodziwika kuti zofuna za moyo wathupi zikonzedwe... kusamala odwala, kusamala zoweta, ndi zina zotere. Tiyesetse kusunga tsiku ili monga momwe Mulungu anapereka zoyenera kucitika pa tsiku ili. Likhale tsiku lopumula thupi ndiponso lopatsa mphamvu za uzimu.



limamva njara kufunafuna zinthu zoyenera pa thupilo ndipo limapeza mayankho ace akupha njara zonsezi.

Monga momwemo mtima wa munthu umamva njara yofuna Mulungu. Njara iyi itiutsa ife kuti tidziwe kuti kuli Mulungu amene angathe kukhutiritsa njara ya mizimu yathu kuti timupeze ndi kum'dziwa Iye.

*"Monga nswala ipuma wefuwefu kukhumba mtsinje, motero moyo wanga upuma wefuwefu kukhumba Inu, Mulungu."* Masalmo 42:1

**3. Cifukwa cakuti munthu amazindikira cimo poonetsa kuti kuli Mulungu amene timamucimwira.**

Tiyeni tiganizire mwa citsanzo monena kuti kunali dziko lina limene linalibe mfumu ndi kale lonse ndipo kunalibe malamulo oweruza dzikolo. Inu mukanatha kulowa m'dzikolo ndikucita ciri conse cokukondweretsani, panalibe amene akananena kuti ndinu woswanya lamulo kapena kuti ndinu mdani wa mfumu. Kunalibe malamulo amene mukanaononga. Kunalibe mfumu imene mukanaicimwira. Motero, payenera kukhala munthu tisanamucimwire ndipo payenera kukhala malamulo tisanawaswanye.

Pamene munthu ayang'anitsitsa mozama mumtima mwace, amadziwa kuti wacimwa. Amadziwa kuti wacita zinthu zimene ziri zolakwa. Amadziwa kuti walephera kucita zabwino zimene akanayenera kucita. Tsopano, popeza wacimwa, payenera kukhala Mulungu wom'cimwirayo. Kuyenera kukhala malamulo a Mulungu amene timawaononga. Kudziwa malamulo a Mulungu kunaikidwa mumtima mwa munthu ndi Mulungu mwini. Cifukwa ca cimeneci cakuti munthu amadziwa kuti wacimwa citiphunzitsa ife kuti kuli Mulungu amene tim'cimwira.

Zoonadi siticita kufuna kukhala ndi Buku Lopatulika kuti tidziwe kuti kuli Mulungu. Mulungu mwini yekha analemba cinthu cimeneci m'mitima ya anthu onse.

*"Popeza iwo aonetsa nchito ya lamulo yolembedwa m'mitima yao."* Aroma 2:15a

## UMODZI

Angakhale kuti siticita kufuna kukhala ndi Buku Lopatulika kuti tidziwe kuti kuli Mulungu, Mulungu anadziwa kuti tiyenera kukhala ndi Mau otizindikiritsa bwino za makhalidwe ace a Mulungu za njira ya cipulumutso, ndi za njira ya moyo wa Cikristu.

Tsopano tidzayamba kuphunzira zinthu zimene Buku Lopatulika litiphunzitsa pa za Mulungu.

Buku Lopatulika litiphunzitsa ife za Umodzi. Ciphunzitso conena za Umodzi (Mulungu ananena monga..."Mulungu Tate, Mulungu Mwana, Ndi Mulungu Mzimu Woyera) ciri cobvuta kucizindikira. Komatu, cinenedwa bwino-bwino m'Buku Lopatulika. Tisamaganiza kuti sicingakhale coonadi cifukwa Masalmo uja anaganiza-ganiza za nzeru yodabwitsa ya Mulungu, iye anazizwa nati, *"Kudziwa ici kundilaka ndi kundidabwitsa: Kundikhalira patali, sindifikilako."* Masalmo 139:6. Ciphunzitso ca Umodzi mwa atatu, sicingazindikirikedi mokwanira bwino, koma ciyenera kulandiridwa ndi kucikhulupirira popeza Buku Lopatulika litiphunzitsa bwino-bwino za cimeneci.

M'buku Lopatulika tiphunzira kuti kuli Mulungu m'modzi yekha ndipo ndi yekhayo, *"Imvani, Israyeli; Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye m'modzi."* Deuteronomo 6:4. Buku Lopatulika litionetsera bwino-bwino, za Mulungu woona m'modzi yekha monga: Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Tiyeni tiyang'anitsitse zina za mau amene amanena za cimeneci.

**1. Buku Lopatulika litiphunzitsa kuti Yesu ndi Atate ndi amodzi.**

*"Ine ndi Atate ndife amodzi."* Yohane 10:30.

*"Iye amene wandiona Ine waona Atate; unena iwe bwanji, Mutionetsere Atate?"* Yohane 14:9b.

*"Ndiko kunena kuti Mulungu anali mwa Kristu, alinkuyanjanitsa dziko lapansi kwa Iye yekha."* 2 Akorinto 5:19a.

**2. Buku Lopatulika litiphunzitsa kuti Yesu ndi Mzimu Woyera ndi amodzi.**

Pamene Yesu ananena za kubwera kwa nkhoswe ina, imene uli Mzimu Woyera, anatanthauza kuti ngati Mzimu Woyera udzakhala pa dziko lapansi lino kudzakhala kofanana ndi monga momwe Yesu akanakhalira pa dziko lapansi lino.

*"Ndipo Ine ndidzapempha Atate, ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe ina, kuti akhale ndi inu ku nthawi zonse ndiye Mzimu wa coonadi; amene dziko lapansi silingathe kumlandira, pakuti silimuona Iye, kapena kumzindikira Iye. Inu mumzindikira Iye; cifukwa akhala ndi inu nakhala mwa inu."* Yohane 14:16-18.



*"Motero Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata."* Marko 2:28

**2. Atakwera kumwamba, Yesu analipobe kudzera mwa Mzimu Woyera monga momwe anaphunzitsira ndi kutsogolera a kuphunzira ace**

*"Koma nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, Iyeyo adzaphunzitsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu."* Yohane 14:26

*"Koma atadza Iyeyo, Mzimu wa coonadi, adzatsogolera inu m'coonadi conse, pakuti sadzalankhula za Iye mwini; koma zinthu ziri zonse adzazimva, adzazilankhula; ndipo zinthu zirinkudza adzakulalikirani."* Yohane 16:13

**3. Akuphunzira, pansi pa utsogoleri wa mzimu woyera anapembedza pa tsiku loyamba la Sabata. Sitiuzidwa cifukwa cace cimene anacitira cimeneci, koma tiuzidwa kuti anatero**

*"Ndipo tsiku loyamba la sabata, posonkhana akuphunzira kunyema mkate, Paulo anawalalikira iwo."* Macitidwe 20:7a

*"Tsiku loyamba la Sabata yense wa inu asunge yekha monga momwe apindulira, kuti zopereka zisacitike pakudza ine."* 1 Akorinto 16:2

Tiona tsopano kuti mipingo ya Cipangano Catsopano inapembedza ndi kubwera ndi zopereka pa tsiku loyamba la sabata. Pamene timpembedza pa tsiku loyamba la sabata, ndiye kuti tiri kupembedza pa tsiku lomwe mipingo ya Cipangano Catsopano inali kupembedza. Munthu amene anena kuti tiri kulakwa, alikunenanso kuti akuphunzira a Cipangano Catsopano anali kulakwa. Tisamvere zokamba zimenezi, koma koposa, tipitirire kutsata citsanzo cimene timapeza m'Mau Opatulika a Mulungu, ndiwo Buku Lopatulika.

## KUSUNGA KWENI-KWENI KWA TSIKU LOYAMBA

Ngakhale kuti tsiku lakupembedza linasinthidwa, cofuna ca munthu cipitirirabe monga momwemo. Afunabe tsiku lopumula ndi kupembedza. Tsiku loyamba la sabata linasanduka tsiku lotero kwa Mkristu.

Mkristu acite ciani pa tsiku ili? Ndiyo nthawi yolalikira uthenga wabwino, kupembedza, ndi kupumula. Mulungu safuna kuti ili

## TSIKU LAKUPEMBEDZA

Yesu ananeneratu momveka bwino kuti tsiku la Sabata linapatsidwa kuti likhale lothandiza zosowa za munthu. *"Ndipo Iye ananena nao, Sabata linaikidwa cifukwa ca munthu, si munthu cifukwa ca Sabata."* Marko 2:27, Tsopano pamene tiwerenga mau a Mulungu, tiona kuti Sabata linaikidwa cifukwa ca zinthu ziwiri pa moyo wa munthu. Kodi zinthu ziwirizi zinali zotani?

**1. Munthu amafuna nthawi yakuti thupi lace lipumure. Mulungu anatanthauza kuti tsiku la Sabata likhale lopumura.**

*"Uzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumaliza nchito zako zonse; koma tsiku la cisanu ndi ciwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire nchito iliyonse."* Eksodo 20:8-10a

**2. Munthu afuna nthawi yopembedza ndi yophunzira za uzimu. Yesu anagwiritsa nchito tsiku la Sabata mwa njira imeneyi ndiponso ngati tsiku lopumula. uwu unali mwambo wace.**

*"Ndipo anadza ku Nazarete, kumene analeredwa; ndipo tsiku la Sabata anaowa m'sugoge, monga anazolowera, naimiriramo kuwerenga m'kalata."* Luka 4:16

Tiona tsopano kuti Mulungu anakonza tsiku la Sabata kukhala nthawi yopumula ndi yopembedza.

## KUSINTHIKA KWA TSIKU LA SABATA KUTI LIKHALE TSIKU LOYAMBA

Monga ife a Baptist, tiyenera kuzindikira bwino cifukwa cakuti timapembedza pa tsiku loyamba la Sabata m'malo mwa kupembedza pa tsiku la cisanu ndi ciwiri. Phunzirani bwino zinthu talembazi:

**1. Kristu ndiye Mbuye wa Sabata**

Monga Mbuye wa Sabata, ali ndi ulamuliro pa ilo angathe kusintha ngati atafuna.



*"Yesu anayankha nati kwa iye, Ngati wina akonda Ine, adzasunga mau anga; ndipo Atate wanga adzamkonda, ndipo tidzadza kwa iye, ndipo tidzayesa kwa iye mokhalamo."* Yohane 14:23

**3. Buku Lopatulika liphunzitsa kuti Mulungu ndi Mzimu Woyera ndi amodzi.**

Petro anaphunzitsa kuti cinyengo ca kwa Mzimu Woyera ciri cinyengo ca kwa Mulungu.

*"Koma Petro anati, Hananiya, Satana anadzaza mtima wako cifukwa ninji kudzanyenga Mzimu Woyera, ndi kupatula pa mtengo wace wa mundawo? Pamene unali nao, sunali wako kodi? Ndipo pamene unaugulitsa sunali m'manja mwako kodi? Bwanji cinalowa ici mumtima mwako? Sunanyenga anthu komatu Mulungu."* Macitidwe 5:3-4

*"Kodi simudziwa kuti muli Kacisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu?"* 1 Akorinto 3:16

Pamene tiganizira za mau tanena pamwambapa, tiona kuti Buku Lopatulika litiphunzitsa ife kuti Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ali amodzi. Kapena citsanzo ici citithandiza kuzindikira kuti m'modzi angathe bwanji kukhala atatu ndi atatu angathe bwanji kukhala m'modzi. Tayang'anani mtengo. Ndi mtengo umodzi, ndipo mtengo umapangidwa ndi mizu, thunthu (thupi la mtengo), ndi masamba. Gawo liri lonse liri ndi nchito yace komabe ziri ziwalo za mtengo umodzi. Mulungu ali Mulungu m'modzi, komabe anadzizindikiritsa yekha mwa umodzi wa Mulungu Tate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera.

## MAKHALIDWE A MULUNGU

Pali zinthu zambiri pa dziko lapansi zimene ziri pamwamba pa nzeru ya munthu; ndipo zilephereka kudzizindikira. Ngati tilephera kuzindikira zinthu zooneka ndi maso pa dziko lapansi lino, sitingathe kuzindikira bwino za Mulungu wamkuru amene analenga dziko lapansi ndi zinthu zonse ziri m'menemo. Koma pali zinthu zina zimene tingathe kudziwa za Mulungu cifukwa zinthu zimenezi anazionetsera kwa ife m'Buku Lopatulika. Cifukwa cace tiyeni tiganizire za zinthu zimene Buku Lopatulika litiphunzitsa za makhalidwe a Mulungu.

**1. Mulungu ali Wamuyaya.**

Ici citanthauza kuti Mulungu alibe mayambiro kapena malekezero. Iye alipo ndipo adzakhala alipobe nthawi zonse.

*"Asanabadwe mapiri, kapena musanalenge dziko lapansi, ndi lokhalamo anthu, Inde, kuyambira nthawi yosayamba kufikira nthawi yosatha, Inu ndinu Mulungu."* Masalmo 90:2

*"Koma Yehova akhala cikhalire."* Masalmo 9:7a,

**2. Mulungu ndi Mzimu.**

Ici citanthauza kuti Mulungu alibe thupi la nyama, kapena mafupa, kapena magazi monga zimene tiri nazo ife.

*"Mulungu ndiye mzimu; ndipo omlambira Iye ayenera kumlambira mu mzimu ndi M'coonadi."* Yohane 4:24

*"Koma Ambuye ndiye Mzimu."* 2 Akorinto 3:17a

**3. Mulungu ndiye Mphamvu Zonse.**

Palibe malire pa mphamvu ya Mulungu. Palibe cosatheka kwa Mulungu.

*"Ndipo Yesu anawayang'ana, nati kwa iwo, Ici sicitheka ndi anthu, koma zinthu zonse zitheka ndi Mulungu."* Mateyu 19:26

*"Cifukwa palibe mau amodzi akucokera kwa Mulungu adzakhala opanda mphamvu."* Luka 1:37

*"Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine kumwamba ndi pa dziko lapansi."* Mateyu 28:18

**4. Mulungu adziwa zonse.**

Mulungu adziwa zinthu zonse. Adziwa zimene zacitika ndipo adziwa zimene zidzacitika mtsogolo. Adziwa zonse zimene ife timacita ndipo adziwa zonse zimene ife timaganiza.

*"Ndipo palibe colembedwa cosaoneka pa maso pace, kona zonse zikhala pambalambanda ndi zobvundukuka pa maso pace pa Iye amene ticita naye."* Ahebri 4:13

*"Ndipo anapemphera, nati, Inu Ambuye, wozindikira mitima ya onse."* Macitidwe 1:24a

**5. Mulungu ali ponse-ponse.**

Kulibe malo kumene munthu angapite kuthawa Mulungu.

*"Ndidzapita kuti kuzembera mzimu wanu? Kapena ndidzathawira kuti kuzembera nkhope yanu? Ndikakwera kunka kumwamba muli komweko; Kapena ndikadziyaira ku Gehena, taonani, muli komweko."* Masalmo 139, 8.



sitingopereka ndalama zoyenera kokha koma tiperekenso ndi mtima woyenera.

***"Yense acite monga anatsimikiza mtima, si mwacisoni kapena mokakamiza, pakuti Mulungu akonda wopereka mokondwera."*** 2 Akorinto 9:7

***"Ndipo ndingakhale ndipereka cuma canga conse kudyetsa osauka, ndipo ningakhale ndipereka thupi langa alitenthe m'moto, koma ndiribe cikondi, sindipingura kanthu ai."*** 1 Akorinto 13:3

*"Tsiku loyamba la Sabata yense wa inu asunge yekha, monga momwe anaipindula, kuti zopereka zisacitike pakudza ine."* 1 Akorinto 16:2

Pamene Mkristu apereka cakhumi cace, ndi mphatso ya kwa Ambuye Yesu Kristu m'mwamba.

*"Ndipo pano anthu ofoka alandira limodzi la magawo khumi; koma apo iye, woti adam'citira umboni kuti ali ndi moyo."* Ahebri 7:8

## UDINDO WATHU

Yesu analankhula mafanizo ambiri ophunzitsa za udindo wa munthu wa nchito kwa mbuye wace ndi m'mene, tsiku lina, wa nchitoyo ayenera kukamba zonse kwa mbuye wace za ukapitao wace. (Werengani mosamala Mateyu 25:14-30.)

Tsiku lina, ifenso tidzafika pa maso pa Yesu Kristu ndi kunena zonse za m'mene tagwiritsira nchito zinthu zonse zimene anatisungitsa ife. Nchito ya ndalama zathu zoonadi siyokhayo imene tiyembekezera kucita komatu ndi gawo la udindo wathu.

*"Komatu pano pafunika za audindo, kuti munthu akhale wokhulupirika."* 1 Akorinto 4:2

*"Pakuti ife tonse tiyenera kuonetsedwa ku mpando wakuweruza wa Kristu, kuti yense alandire zocitika m'thupi, monga momwe anacita, kapena cabwino kapena coipa."* 2 Akorinto 5:10

## MWAI WATHU

Kukhala woyang'anira cikadayenera kukhala ngati mwai wathu waukuru. Citipatsa mwai wakucita nao pa nchito ya Mulungu. Ndiponso, padzakhala mphotho kwa iwo amene ayesetsa kukhala oyang'anira abwino.

*"Pakuti ife ndife a nchito anzace a Mulungu."* 1 Akorinto 3:9a

*"Mbuye wace anati kwa iye, Cabwino kapolo iwe wabwino ndi wokhulupirika; unali wokhulupirika pa zinthu zazing'ono, ndidzakhazika iwe pa zinthu zambiri; lowa iwe m'cikondwerero ca mbuye wako."* Mateyu 25:23

## MAKHALIDWE ATHU

Mulungu sakondwera ndi zithu zokha zimene ticita kapena ndalama zimene tipereka. Amakondweranso ndi makhalidwe athu m'mene ife titumikira ndi kupereka. Tiyeni tionetsetse kuti



*"Pakuti Ine Yehova sindisinthika."* Malaki 3:6a.

*"Yesu Kristu ali yemweyo dzulo, ndi lero, ndi ku nthawi zonse."* Ahebri 13:8

**7. Mulungu ali woyera.**

Mulungu adana ndi cimo ndipo acokapo pa cinthu ciri conse cimene ciri cimo.

*"Ndipo wina anapfuula kwa mnzace, nati, Woyera, Woyera, Woyera, Yehova wa makamu; dziko lonse lapansi ladzala ulemelero wace."* Yesaya 6:3

*"Ndani adzakhala wosaopa ndi wosalemekeza dzina lanu Ambuye? Cifukwa Inu nokha muli woyera."* Cibvumbulutso 15:4a.

**8. Mulungu ali Wolungama.**

Ici citanthauza kuti Mulungu adana nalo cimo ndipo akonda cimene ciri cabwino. Cifukwa Mulungu ali wolungama, afuna cilungamo mwa munthu.

*"Yehova ali wolungama m'njira zace zonse, ndi wacifundo m'nchito zace zonse."* Masalmo 145:17

*"Kuti aonetse cilungamo cace m'nyengo yatsopano; kuti Iye akhale wolungama, ndi wakumuyesa wolungama iye amene akhulupirira Yesu."* Aroma 3:26

**9. Mulungu ali Wacilungamo.**

Ici citanthauza kuti Mulungu amene adana nalo cimo nakondwera naco cilungamo afuna athu onse asungidwe mwa cilungamo. Anthu amacita cimo limene salandira nalo cilango pansi pano. Mulungu adzafuna kuti cilungamo cicitike pa tsiku loweruza.

*"Pakuti akudza, pakuti akudza kudzaweruza dziko lapansi: Adzaweruza dziko lokhalamo anthu ndi cilungamo."* Masalmo 96:13

*"Ndipo tidziwa kuti kuweruza kwa Mulungu kuli koona kwa iwo a kucita zotere."* Aroma 2:2

**10. Mulungu ndiye Cikondi.**

Mulungu akonda anthu onse, Koma cikondi ici sicimuphimba m'maso Mulungu kuti Iye sangathe kuona nchito zoipa za munthu. Kapenanso kuti cikondi cimeneci cingamuletse kuweruza mwa cilungamo kwa iwo amene akonda kukhala ndi

kufa m'macimo awo, ai. Cikondi ca Mulungu ndico cinamkakamiza Iye kutumiza Mwana wace, Yesu Kristu, kudzafera macimo a anthu onse. Imfa ya Yesu ya pa mtanda cifukwa ca macimo athu ipatsa mwai kwa anthu kuti alandire cikhululukiro ca macimo ndi moyo wosatha. Kulandira cikhululukiro ici, munthu ayenera kulapa mumtima mwace nakhulupirira Kristu kuti ndiye Mpulumutsi wace.

*"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa Yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike koma akhale nao moyo wosatha."* Yohane 3:16

*"Koma Mulungu atsimikiza kwa ife, cikondi cace ca mwini yekha m'menemo, kuti pokhala ife cikhalire ocimwa Kristu adatifera ife."* Aroma 5:8



*"Ndipo taonani, ndawaninkha ana a Levi limodzi la magawo khumi mwa zonse m'Israyeli, likhale colowa cawo, mphotho ya pa nchito yao alikuicita, nchito ya cihema cokomanako."* Numeri 18:21

Timamvanso za makhalidwe a Mulungu pamene anthu analephera kumvera lamulo ili.

*"Kodi munthu adzalanda za Mulungu? Ndipo inu mundilanda Ine. Koma mukuti, Takulandani zotani? Limodzi la magawo khumi, ndi zopereka. Mutemberedwa ndi temberero; pakuti mundilanda Ine, ndi mtundu uwu wonse. Mubwere nalo limodzi limodzi lonse la khumi, ku nyumba yosungiramo, kuti m'nyumba mwanga mukhale cakudya; ngati sindikutsegulirani mazenera a kumwamba, ndi kukutsanurilani mdalitso wakuti adzasowa malo a kuulandira."* Malaki 3:8-10

**KUNKHALA WOYANG'ANIRA MONGA ANAPHUNZITSA YESU**

Zoonadi Yesu anapereka cakhumi pakuti Iye anakwaniritsa lamulo.

*"Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula cilamulo kapena aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa."* Mateyu 5:17

Yesu anabvomereza kupereka ca cikhumi, komanso pomwepo, Iye anakumbutsa anthu kuti pali zambiri zofunika pa cipembedzo osati ca cikhumi cokha.

*"Tsoka inu, alembi ndi afarisi, onyenga! cifukwa mupereka limodzi la magawo khumi la timbeu tonunkhila, ndi katsabola, ndi la citowe, nimusiya zolemera za cilamulo, ndi kuweruza kolungama, ndi kucitira cifundo, ndi cikhulupiriro; koma zimenezi munayenera kuzicita, osasiya izi zosacitidwa."* Mateyu 23:23

**3. Kuyang'anira kophunzitsidwa mu makalata.**

Akristu ayenera kuthandiza mbusa kuti iye apereke nthawi yace yonse ku nchito imene Mulungu anamuitanira.

*"Comweconso Ambuye analamulira kuti iwo amene alalikira Uthenga Wabwino akhala ndi moyo ndi Uthenga Wabwino."* 1 Akorinto 9:14

Akristu ayenera kupereka kutsatana ndi njira imene Mulungu wa wakonzera iwo ndipo ayenera kucita kawiri-kawiri pa tsiku loyamba la Sabata.

## KUYANG'ANIRA

Oyang'anira ndi munthu amene wapatsidwa udindo wosunga katundu wa munthu wina. Iye ayembekezedwa kusunga ndi kugwiritsa nchito katunduyo mwa njira yokondweretsa mwini wace. Mulungu ndiye mwini wace wa zinthu zonse. Zinthu zimene ziri ndi ife zinapatsidwa kwa ife ndi Mulungu. Tizigwiritse nchito zinthu izi m'njira yakuti Mulungu adzakondwera nayo. Ukapitao wabwino ndiko kugwiritsa nchito bwino kwa zinthu zimene zinapatsidwa kwa ife.

Pakuti Mkristu, zinthu zonse, ndi moyo womwe, ndi ukapitao wocokera kwa Mulungu.

*"Kapena simudziwa kuti thupi lanu liri kacisi wa Mzimu Woyera, amene ali mwa inu, amene muli naye kwa Mulungu, ndipo simukhala a inu nokha? Pakuti munagulidwa ndi mtengo wace wa patali: cifukwa cace lemekezani Mulungu m'thupi lanu, mu mzimu wanu zimene ziri za Mulungu."* 1 Akorinto 6:19, 20

Mkristu amene ali woyang'anira wabwino agwiritse nchito nthawi yace, makhalidwe ace, cikoka codziwana bwino ndi ena, cuma cace, ndi zinthu zonse cifukwa ca ulemelero wa Yesu Kristu. Mu phunziro ili tifuna maka-maka kuganizira ukapitao wa pa cuma cathu.

## KUKHALA WOYANG'ANIRA M'BUKU LOPATULIKA

**1. Kuyang'anira m'cipangano ca kale.**

Tiphunzira kuti zinthu zonse ndi za Mulungu.

*"Paciyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi."* Genesis 1:1

*"Pakuti za moyo zonse za kuthengo ndi zanga, ndi ng'ombe za pa mapiri zikwi."* Masalmo 5:10

*"Siliva ndi wanga, golidi ndi wanga, ati Yehova wamakamu."* Hagai 2:8

Timamvanso kuti Mulungu analamulira anthu ace kupereka cakhumi cothandiza nchito ya Mulungu.

*"Limodzi mwa magawo khumi la zonse m'dziko, la mbeu zace za dziko, la zipatso za mtengo, ndilo la Yehova; likhale lopatulikira Yehova."* Levitiko 27:30





## AMBUYE YESU KRISTU

Pa mutu uwu tidzakhala tiri kuphunzira zoonadi zinai za Yesu Kristu. Tidzaona kuti Buku Lopatulika litiphunzitsa kuti Yesu ali Mwana wopatulika wa Mulungu.

## YESU MONGA MULUNGU

Sicokwanira kungonena kuti Yesu anali mphunzitsi wamkuru, mneneri wamkuru, wa nchito zodabwitsa. Zoonadi anali wa zonsezi, koma anali woposa pamenepa, Yesu anali Mwana wa Mulungu wopatulika.

**1. Umulungu wace uonekera pa zocita zace.**

*"Zonse zinalengedwa ndi iye, ndipo kopanda Iye sikunalengedwa kanthu kali konse kolengedwa."* Yohane 1:3

*"Pakuti mwa Iye zinalengedwa zonse za m'mwamba ndi za pa dziko."* Akolose 1:16a.

**2. Umulungu wace uonekera pa kufanana kwace ndi Mulungu.**

Monga Mulungu ali wamuyaya comweco Yesu ali wamuyaya.

*"Paciyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu ndipo Mau ndiye Mulungu."* Yohane 1:1

M'mau a Mulungu awa pamene anena kuti "Mau likhala ngati dzina lina la Yesu."

Yesu anaphunzitsa kuti Iye ayenera kulemekezedwa monga momwe alemekezedwera Atate. *"Kuti onse akalemekeze Mwana, monga alemekeza Atate."* Yohane 5:23a

Yesu anaphunzitsa kuti anthu akhulupirire Iye monga momwe akhulupirira Mulungu. *"Mtima wanu usabvutike; mukhulupirira Mulungu, khulupirirani Inenso."* Yohane 14:1.

**3. Umulungu wace uonekera pa nchito zace za mphamvu zimene anacita.**

Yesu analamulira mphepo ndi nyanja pa nthawi ya mafunde. *"Pomwepo Iye anauka, nadzudzula mphepo ndi nyanja, ndipo panagwa bata lalikuru."* Mateyu 8:26b

Yesu anali kuturutsa ziwanda. *"Ndipo Yesu anadzudzula, kuti, Khala uli cete, nuturuke mwa iye. Ndipo mzimu wonyatsa, pom'ng'amba ndi kupfuula ndi mau akuru, unaturuka mwa iye."* Marko 1:25, 26

Yesu anaciritsa nthenda zazikuru ndi mau okha. Pa ndime iyi tidzaphunzira za m'mene Yesu anaciritsira munthu amene anakhala wosayenda pa zaka makumi atatu kudza mphambu zisanu ndi zitatu (38). *"Yesu ananena naye, Tauka, yalula mphasa yako, nuyende. Ndipo pomwepo munthuyu anacira."* Yohane 5:8. 9a.

Yesu anali kubwezera moyo kwa akufa. m' Cipangano ca Tsopano tiuzidwa nthawi zitatu zimene Yesu anaukitsa anthu akufa. Mau awa, amene tiri kufuna kunena tsopano linowa, atiuza za *munthu amene anaukitsidwa kwa akufa patapita masiku anai. "Ndipo mmene adanena izi, anapfuula ndi mau akuru Lazaro, tuluka ndipo womwalirayo anatuluka."* Yohane 11:43, 44a

Citsimikizo cacikuru ca Umulungu wa Yesu ndico ca kuuka kwa akufa kwace. Yesu atafa pa mtanda anaikidwa m' manda. Tsiku la citatu la imfa yace. Yesu anauka kuturuka m'manda ndipo anadzionetsera nthawi zambiri kwa akuphunzira ace asanakwere kunka kumwamba. Mau amene tidzanena munsimuwa adzatithandiza kuzindikira tanthauzo lace leni-leni la kuuka kwa akufa kwace kwa Yesu mwakusonyeza Umulungu wace. *"Amene anatsimikizidwa ndi mphamvu kuti ndiye Mwana wa Mulungu monga mwa mzimu waciyero, ndi kuuka kwa akufa."* Aroma 1:4

## YESU MONGA MUNTHU

Sitiphunzitsidwa kuti Yesu anali Mwana Wopatulika wa Mulungu kokha koma tiphunzitsidwanso kuti Yesu anali munthu. Iye anali ndi mnofu nakhala pa dziko lapansi monga munthu ngati inu ndi ine.

**1. Umunthu wace uonekera pa kubadwa kwace.**

Yesu akanatha kubwera kumwamba monga ngati munthu wamkuru kale, koma kunali kufuna kwace kukhala monga tiriri ife. Mmalo mokwaniritsa cinthu ici, Iye anabadwa mwa mkazi monga ticita anthu tonse Atate wace anali Mulungu koma Yesu analowa m' mimba ya namwali, Mariya. Ndipo anabadwa ku dziko lapansi monga mwana wakhanda.

*"Koma Mariya anati kwa mngelo, Ici cidzacitika bwanji popeza ine sindidziwa mwamuna? Ndipo mngelo anayankha, nati kwa iye, Mzimu Woyera adzafika pa iwe, ndi mphamvu ya Wamkulukulu idzakuphimba iwe; cifukwa cacenso Coyeneraco cikadzabadwa, cidzachedwa Mwana wa Mulungu."* Luka 1:34, 35



## MASUNGIDWE A MGONERO WA AMBUYE

Nthawi zambiri pali funso lofunsa kuti mgonero uzicitika kangati. Buku Lopatulika silitiuza kanthu. Ndi cinthu cakuti mpingo uli wonse ukhoza kudzinganizira wokha. Uyenera kucitika kawiri-kawiri kuti tisunge coonadi cacikuru cimene utiphunzitsa kuti cikhazikike m' miyoyo ndi m' mitima yathu. Sitiyenera kucita nthawi zambiri-mbiri kuti cingakhale ngati cizolowezi cacabe ndi kulephera kuzindikira coonadi cace.

Masungidwe a mgonero sayenera kutengedwa mopepuza. Payenera kukhala kukonzekera bwino mwa uzimu kwa munthu aliyense isanafike nthawi yoyandikira ku mgonero.

*"Koma munthu adziyese yekha, ndi kotero adye mkate ndi kumwera cikho. Pakuti iye wakudya ndi wakumwa adya namwa ciweruzo kwa iye yekha, ngati sazindikira thupilo."* 1 Akorinto 11:28, 29

## CIZINDIKIRO CA MGONERO WA AMBUYE

Anthu ena amaphuzitsa kuti mkate ndi vinyo zimasanduka thupi leni-leni ndi mwazi weni-weni wa Yesu. Anena kuti mkate ndi vinyo sizidzindikiro za thupi ndi mwazi wa Yesu ai, koma kuti izi zimasandukadi thupi ndi mwazi wa Yesu. Pakuphunzira Mau a Mulungu cidzatiululira ife kuti Yesu ananena za mkate ndi vinyo monga zidzindikiro za thupi lace ndi mwazi wace. Tiwerenge za Mgonero wa Ambuye mu 1 Akorinto 11:24-26.

*"Ndipo m'mene adayamika, ananyema, nati, Ici ndi thupi langa la kwa inu; citani ici cikhale cikhumbukiro canga. Koteronso cikho, citatha cakudya, ndi kuti, Cikho ici ndi pangano latsopano m'mwazi wanga; citani ici, nthawi zonse mukamwa, cikhale cikumbukiro canga. Pakuti nthawi zonse inu mukadya mkate uwu ndi kumwera cikho, mulalikira imfa ya Ambuye kufikira akadza Iye."* 1 Akorinto 11:24-26

Onetsetsani mosamala...pa gawo loyamba la mauwa, Yesu analankhula za makate ndi vinyo nati, "Ici ndi thupi langa," ndiponso "Cikho ici ndi pangano latsopano m'mwazi wanga." Ayenera kukhala atatanthauza kuti izi zinali zidzindikiro za zinthu zimenezi cifukwa pambuyo pace akunena kuti, "...nthawi zonse mukadya mkate uwu ndi kumwera cikho..." Apa palibe cokaikitsa...unali mkate ndithu ndi vinyo ndithu. Yesu sanasinthe mkate kukhala thupi lace kapena vinyo kukhala mwazi wace. Anagwiritsa nchito zinthu izi monga zidzindikiro za thupi lace losweka pa mtanda ndi mwazi wace wokhetsedwa pa mtanda.

## CIFUKWA CACE CA KUCITA MGONERO

**1. Mgonero wa Ambuye ucitika kusunga cikumbukiro ca Iye.**

Yesu anati; *"Citani ici cikhale cikumbukiro canga."* 1 Akorinto 11:24b. Pamene tidya mgonero tikumbukira mwa njira ina mmene thupi la Yesu linaswekera ndi m'mene mwazi wace unakhetsedwera kuti tikhale ndi moyo.

**2. Mgonero wa Ambuye uonetsa imfa ya pa mtanda ya Ambuye Yesu.**

*"Mulalikira imfa ya Ambuye kufikira akadza Iyeyo."* 1 Akorinto 11:26b. Palibe coyenereza pakudya mgonero malinga kuti maganizo athu atembenukira zimene anaticitira pa mtanda.



**2. Umunthu wace uonekera pa zimene anazimva m'thupi mwace monga zomwe tizimva ife.**

Yesu anamva cisoni pa kumwalira kwa bwenzi lace monga momwe timamvera ife. *"Yesu analira."* Yohane 11:35

Yesu anakula monga momwe timakulira ife. *"Ndipo Yesu anakulabe m'nzeru ndi mu msinkhu, ndi m'cisomo ca pa Mulungu ndi ca pa anthu."* Luka 2:52

Yesu anali kuyesedwa monga tiyesedwera ife. *"Koma wayesedwa m'zonse monga momwe ife, koma wopanda ucimo."* Ahebri 4:15b

**3. Umunthu wace uonekera pakumva kuwawa kwace kumene anamva pa mtanda. Werengani mbiri ya kupacikidwa pa mtanda m'mauthenga abwino ndipo werengerani zina za njira zimene Yesu anamvera kuwawa m'thupi.**

## YESU MONGA MPULUMUTSI

**1. Cifukwa cimene Yesu anabwerera ku dziko lapansi cinali cakuti adzatipulumutse ife.**

Ndi zoona kuti Yesu analalikira mau odabwitsa ambiri, anaphunzitsa anthu za Mulungu, ndipo anacita zozizwitsa zambiri pa nthawi imene anali pa dziko lapansi. Koma Iye sanabwere ku dziko lapansi kudzangocita zinthu izi. Iye anabwera kuti adzatipulumutse ife ku macimo athu.

*"Ndipo adzabala mwana wamwamuna, ndipo udzamucha dzina lace YESU: pakuti Iyeyo adzapulumutsa anthu ace ku macimo ao."* Mateyu 1:21

*"Monga mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira, ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri."* Mateyu 20:28

**2. Yesu yekha ndiye Mpulumutsi.**

Pali anthu ambiri amene amaganiza kuti ngati munthu ali wokhulupirika ku cipembedzo cace, zoonadi munthu ameneyo adzapulumuka. Buku Lopatulika linena momveka bwino kuti kulibe cipulumutso kopanda Yesu Kristu.

*"Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo. Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine."* Yohane 14:6.

*"Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo."* Macitidwe 4:12

**3. Njira ya Yesu yakutipulumutsira ife inali pakufa pa mtanda.**

Tiyenera kuzindikira kuti panalibe njira ina yotheka ya cipulumutso. Ngati munthu anali wakuti apulumutsidwe, Yesu, Mwana wa Mulungu wosacimwa, anayenera kufa m'malo mwa munthu wocimwa.

*"Ndipo anamuka patsogolo pang'ono, nagwa nkhope yace pansi, napemphera, nati, Atate, ngati nkutheka, cikho ici cindipitirire Ine; koma simonga ndifuna Ine, koma Inu."* Mateyu 26:39

*"Ndipo wopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka."* Ahebri 9:22

*"Kristu anatiombola kutemberero la cilamulo, atakhala temberero m'malo mwathu; pakuti kwalembedwa, Wotembereredwa aliyense wopacikidwa pamtengo."* Agalatiya 3:13

*"Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse."* Yesaya 53:6

## YESU MONGA AMBUYE

**1. Yesu ali ndi mphamvu zonse kumwamba ndi pa dziko lapansi.**

*"Ndipo Yesu anadza nalankhula nao, nanena, Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine kumwamba ndi pa dziko lapansi."* Mateyu 28:18

**2. Yesu ndi Ambuye a Mkristu aliyense.**

*"Pamenepo lizindikiritse ndithu banja liri lonse la Israeli kuti Mulungu anamuyesa Ambuye ndi Kristu, Yesu amene inu munampacika."* Macitidwe 2:36

*"Kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu, ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu anamuukitsa kwa akufa, udzapulumuka."* Aroma 10:9

**3. Yesu adzazindikiridwa monga Mbuye ndi anthu onse.**

Ngakhale kuti anthu ambiri akana Umbuye wa Yesu, tsiku lina adzabvomereza kuti Yesu ndi Ambuye. Ngati munthu wakana Yesu pamene ali ndi moyo pa dziko lapansi pano, motero Yesu adzamkana iye pa tsiku limenelo. Mateyu 10:32-33

*"Kuti m'dzina la Yesu bondo liri lonse lipinde, la za m'mwamba ndi za padziko, ndi za pansi pa dziko, ndi malilime onse abvomere kuti Yesu Kristu ali Ambuye, kucitira ulemu Mulungu Atate."* Afilipi 2:10, 11



Poyamba pa phunziro ili tanena kuti ubatizo usonyeza imfa, kuikidwa m'manda, ndi kuuka kwa akufa. Kuwaza madzi ndi kuthira madzi pa mutu sidzingasonyeze kuikidwa m'manda. Pamene munthu aikidwa m'manda, aikidwa patali pansi pa nthaka. Ife tisonyeza cimeneci pamene munthu aikidwa pansi pa madzi.

Yesu pa ubatizo anatanthauza kuphunzitsa coonadi cacikuru...imfa ya ku ucimo ya okhulupirirayo mwa Mristu, kuikidwa m'manda kwa okhulupirirayo kunjira ya kale ya moyo wace, ndi moyo watsopano wouka kwa akufa mwa Kristu. Ici cingaonetsedwe pokha-pokha pamene timiza wokhulupirirayo m'madzi ndipo ndi kumuturutsa m'madzimo.

## MUNTHU WOYENERA UBATIZO

Pamene tadzindikira tanthauzo lace leni-leni la ubatizo pamenepo palibe cobvuta poganizira oyenera kubatizidwa. Ubatizo usonyeza kudzindikira za uzimu ndi Yesu Kristu. Iwo okha amene adzindikira cimeneci ndiwo ayenera kuonetsa cimeneci m'madzi a ubatizo. M'cipangano Catsopano tipeza kuti iwo amene analapa nakhulupirira Kristu anabatizidwa. Mu lamulo lace la kwa ife, Yesu anena kuti tipange akuphunzira, ndi kuwabatiza.

*"Pamenepo iwo amene analandira mau ace anabatizidwa."* Macitidwe 2:41a

*"Kodi pali munthu akhoza kuletsa madzi, kuti asabatizidwe awa, amene alandira Mzimu Woyera ngatinso ife?"* Macitidwe 10:47

## MGONERO WA AMBUYE

Lamuro laciwiri limene Yesu anapereka ndilo Mgonero wa Ambuye. Tiyenera kufika kukuzindikira kweni-kweni za zoonadi izi zonena za Mgonero wa Ambuye.

## CIYAMBI CA MGONERO WA AMBUYE

Yesu mwini yekha ndiye anayamba lamulo ili pakupereka mgonero kwa akuphunzira ace asanapacikidwe pa mtanda.

*"Ndipo pamene iwo anali nkudya, Yesu anatenga mkate naudalitsa, naunyema, ndipo m'mene anapatsa kwa ophunzira, anati, Tengani, idyani, ici ndi thupi langa. Ndipo pamene anatenga cikho, anayamika, napatsa iwo, nanena, mumwere ici inu nonse; pakuti ici ndi mwazi wanga wa pangano, wothiridwa cifukwa ca anthu ambiri ku kucotsa macimo."* Mateyu 26:26-28

Pali kusabvomerezana pakati pa mipingo ponena za njira yeni-yeni ya macitidwe a ubatizo. Mipingo ina amathira madzi pa mutu. Mipingo ina imawaza madzi pang'ono pa munthuyo. Mipingo ina ikuti sikufunika konse kucita ubatizo. Ife a Baptist tikuti ubatizo ndiofunika cifukwa ndi cinthu cimene Yesu anatilamulira kuti tizicita. Ndipo ngati tiyenera kubatiza, tiyenera kucita m'njira yomweyo imene inacitika m'Cipangano Catsopano. Tifuna kuti inu mupenyetsetse pa zifukwa zitatu zonena kuti kumiza ndiwo macitidwe amodzi okha a mau a Mulungu pa ubatizo.

**1. Kumiza ndiwo macitidwe eni-eni a ubatizo cifukwa ca tanthauzo la mau onena kuti 'batiza'.**

Pamene Buku Lopatulika linali kumasulidwa kucokera ku Cihelene ndi kulemba mu Cizungu, mau a Cihelene onena kuti 'batizo' mu Cizungu alemba kuti 'batiza'. Ngati tifuna kupeza tanthauzo lace leni-leni la mau amenewa tiyenera kuona mabuku omasulira a Cihelene (Greek dictionary). Litiuza kuti mau onena kuti 'baptidzo' atanthauza kuti: kuika m'madzi thupi lonse, kumiza. Tanthauzo lomweli la mau awa liletsa kuwaza madzi kapena kuthira madzi pa mutu pa munthu. Tiyenera kumiza.

**2. Zitsano za m'Buku Lopatulika zitionetsa ife kuti kumiza ndiyo njira yeni-yeni ya macitidwe a ubatizo.**

*"Ndipo kunali masiku omwewo, Yesu anadza kucokera ku Nazarete wa ku Galileya, nabatizidwa ndi Yohane m'Yordano. Ndipo pomwepo, alinkukwera poturuka m'madzi, anaona Iye thambo litang'ambika, ndi Mzimu alikutsika pa Iye monga nkhunda."* Marko 1:9,10. (Onani mau anena kuti "kuturuka m'madzi."

*"Ndipo Yohane analinkubatiza m'Ainoni pafupi pa Salemu, cifukwa panali madzi ambiri pamenepo."* Yohane 3:23a. (Madzi ambiri siafunika ngati munthu ayenera kungowazidwa kaya kuthiridwa madzi.)

*"Ndipo anamuuza kuti aimitse gareta; ndipo anatsikira onse awiri ku madzi, Filipo ndi mdindoyo; ndipo anambatiza iye."* Macitidwe 8:38

**3. Kumiza ndiwo macitidwe eni-eni a ubatizo cifukwa nkofunika kuonetsa citunzi ca imfa, kuikidwa m'manda, ndi kuuka kwa akufa.**





## MZIMU WOYERA

Kawiri-kawiri pali kusamvana pakati pa Akristu ponena za makhalidwe ndi nchito ya Mzimu Woyera. Ambiri a ife tinamva za fanizo lija la anthu akhungu anai amene anapita kuti akadziwe bwino-bwino za njobvu. Munthu aliyense anakhudza mbali imodzi ya thupi la njobvu naganiza mwa iye yekha m'mene njobvu iliri. Pambuyo pace, pamene anali kukambilana za njobvu, kusutsana kwakukuru kunayambika. Munthu wakhungu amene anakhudza m'mbali mwa thupi la njobvu ananena kuti njobvu ili ngati cipupa. Wina amene anakhudza mwendo wace anasutsa nanena kuti njobvu ili ngati mtengo. Wacitatu, amene anakhudza mcira wace wa njobvu analimbika kuti njobvu ili ngati ntambo. Wotsiriza anakhuza citambo ca njobvu, ndipo anakhulupirira kuti njobvu ili ngati njoka. Tioneratu tsopano kuti kusamvanaku kunabwera cifukwa aliyense anakhudza mbali imodzi ya njobvu.

Kusamvana kwambiri pa za Mzimu Woyera kumabwera m'njira yomweyi. Pamene tigwiritsa nchito malemba a Mau a Mulungu amene aphunzitsa gawo limodzi la makhalidwe ndi utumiki wa Mzimu Woyera ndi kukhala osasamala magawo ena, zoonadi kuli kodziwikiratu kuti padzakhala kusamvana kudzabuka. Kudzakhala kosatheka kuphatikiza mau onse onena za Mzimu Woyera mu phunziro ili. Tayesera, mwa pang'ono kusankha mau ena amene adzatha kupereka cithunzi colinganizika ndiponso utumiki wa Mzimu Woyera.

### UMULUNGU WA MZIMU WOYERA

Pa phunziro lathu la umodzi (Onani Mutu 2.) tinaphunzira kuti Mzimu Woyera ndi amodzi ndi Mulungu Tate ndi Mulungu Mwana. Phunziraninso Mau a Mulungu amenewa mosamala. Tiona tsopano kuti Mzimu Woyera ndi wa Mulungu.

Mzimu Woyera ngosaoneka, ngopatulika, ngwamphamvu zonse, nthawi zonse ulipo, kudzionetsera kwa Mulungu mwini mwa uzimu. Buku Lopatulika litiphunzitsa kuti kudzera mwa Mzimu Woyera Mulungu ndi Yesu akhala mwa Mkristu ndipo akhala ndi iye nthawi zonse.

## MAKHALIDWE A MZIMU WOYERA

Tisanaganize za Mzimu Woyera ngati cinthu.' Mzimu Woyera ndi munthu. Tingathe kucimwira, kunena bodza, ndi kumvetsa cisoni Mzimu Woyera. Sitingacimwire, sitinganenere bodza, ndipo sitingamvetse cisoni 'cinthu ca cabe'....koma munthu yekha.

*"Koma iwo anapadukira ndi kumvetsa cisoni Mzimu wace Woyera."* Yesaya 63:10a

*"Cifukwa cace ndinena kwa inu, Macimo onse, ndi zonena zonse zamwano, zidzakhululukidwa kwa anthu."* Mateyu 12:31

*"Koma Petro anati, Hananiya, Satana anadzaza mu mtima mwako cifukwa ninji kudzanyenga Mzimu Woyera, ndi kupatula pa mtengo wace wa mundawo?"* Macitidwe 5:3

*"Ndipo musamvetse cisoni Mzimu Woyera wa Mulungu amene munasindikizidwa cizindikiro mwa Iye, kufikira tsiku la maomboledwe."* Aefeso 4:31

## NCHITO YA MZIMU WOYERA

Pophunzira za Cipangano ca Kale cidzaonetsera mwamsanga kuti Mzimu Woyera unali kugwira nchito kwambiri m'miyoyo ya anthu asanabwere Yesu ku dziko lapansi. Mulungu anaika Mzimu wace pa anthu ena kuwapatsa mphamvu kuti agwire nchito. Werengani za Gideoni (Oweruza 6:34) Samsoni (Oweruza 14:6.) Davide (1 Samueli 16:13.) Tipeza kuti anthu awa anapatsidwa Mzimu wa Mulungu cifukwa ca nchito imodzi...kutumikira Mulungu.

Ndiponso, pamene tiphunzira za moyo wa Yesu, tiona kuti Mzimu wa Mulungu unatsika monga nkhunda pa ubatizo wace wa Yesu nukhala pa Iye. Yohane anati, *"Ndinaona Mzimu uli Kutsika kucokera kumwamba monga nkhunda; nukhala pa Iye."* (Yohane 1:32.) Yesu anaphunzitsa nayenso kuti nchito zazikuru zimene Iye anacita zinali kucitika ndi mphamvu ya Mzimu wa Mulungu. *"Koma ngati Ine nimaturutsa ziwanda ndi mphamvu yace ya Mzimu wa Mulungu, pomwepo Ufumu wa Mulungu unafika pa inu."* Mateyu 12:28

Pa phunziro ili, poyamba tiyenera kukhudza kwambiri za nchito ya Mzimu Woyera m'miyoyo ya anthu a masiku ano. Pali mau amene amakonzeratu motsiriziratu za nchito ya Mzimu Woyera



**1. Ubatizo ndi macitidwe oonetsa kumvera ku lamulo la Yesu Kristu.**

*"Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera."* Mateyu 28:19

**2. Ubatizo uli mboni kwa onse openyerera. Uwauza kuti inu tsopano muli akufa ku ucimo mwa Kristu ndipo kuti muli ndi moyo watsopano mwa iye.**

## TANTHAUZO LA UBATIZO

1. Poyamba pa zonse, tiyenera kuzindikira kuti ubatizo ndi cizindikiro. Sicipulumutso, koma uzindikiritsa kapena kuti uonetsa cithunzi cacipulumutso cimene cilowa mu mtima mwa okhulupirirayo. Ticenjerepo kuti tisasokoneze cizindikiro ndi cinthu cimene cimazindikiritsa. Munthu angathe kuonetsa cithunzi ndikunena kuti. "Awa ndi mai anga." Pomwepo tikadazindikirira kuti cipeparaco sindico mai wa munthuyo koma ndi cithunzi ca mai wace. Monga momwemo, ubatizo si imfa, sikuikidwa m' manda ndi kuuka, koma ndi cizindikiro kapena kuti cithunzi cace.

2. Ubatizo usonyeza (kapena kuti uonetsa) cithunzi ca imfa, kuikidwa m'manda ndi kuuka; zimene wokhulupirirayo abvomereza mumtima mwace kudzera mwa cikhulupiriro ca mwa Yesu Kristu.

*"Cifukwa cace tinaikidwa m'manda pamodzi ndi Iye mwa ubatizo kulowa mu imfa; kuti monga Kristu anaukitsidwa kwa akufa mwa ulemerero wa Atate, cotero ifenso tikayende m'moyo watsopano."* Aroma 6:4

Pali mau akuru-akuru atatu m'ndime iyi amene tiyenera kuwaganizira mwacidule...imfa, kuikidwa m'manda, kuuka kwa akufa.

Pamene wokhulupirirayo alandira Yesu kuti ndiye Mpulumutsi, alandira imfa ya Kristu ngati imfa yace ya ku ucimo. Cifukwa cace, mwa Kristu, anafa mu ucimo. Watha (monga munthu wakufa) ku njira yace yakale ya moyo wace. Alandira moyo watsopano mwa Kristu. Ubatizo usonyeza imfa iyi, kuikidwa m'manda ndi kuuka kwa akufa.

MUTU 8

## MALAMULO A MPINGO

Pamene tiphunzira za Cipangano Catsopano tipeza kuti Yesu anapatsa mpingo malamulo awiri amene anali oyenera kusungidwa. Lamulo limodzi la malamulo awiriwa liphunzitsa coonadi cacikuru ca Uthenga Wabwino. Moyo wa uzimu wa mipingo yathu udzalimbikitsidwa kwambiri kudzera mwa kuzindikira bwino ndi kusunga malamulo awiriwa. Tiyeni poyamba tiganizire lamulo la ubatizo.

## UBATIZO
## UBATIZO SIUPULUMUTSA

Mwatsoka, kudzera mwakusazindikira Mau a Mulungu anthu ena amaganiza kuti ubatizo uli wofunika pa cipulumutso. Tizindikire bwino-bwino kuti ubatizo siupulumutsa.

**1. Ubatizo siupulumutsa cifukwa kuti madzi sangatsuke cimo...mwazi wa Yesu okha ndiwo ungacite cimeneci.**

*"...Ndipo mwazi wa Yesu Mwana wace utisambitsa kuticotsera ucimo wonse."* 1 Yohane 1:7b

**2. Ubatizo siupulumutsa cifukwa ndi cocita munthu, koma cipulumutso ndi mphatso ya Mulungu.**

*"Pakuti muli wopulumutsidwa cifukwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu; ciri mphatso ya Mulungu, cosacokera ku nchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense."* Aefeso 2:8, 9.

**3. Tidziwa kuti ubatizo siupulumutsa cifukwa mbala pa mtanda paja inapulumutsidwa ndi cisomo ca Mulungu popanda ubatizo.**

*"Ndipo Iye ananena naye, Indetu, ndinena ndi iwe, lero lino udzakhala ndi ine m'Paradaiso."* Luka 23:43

## KUFUNIKA KWA UBATIZO

Pali anthu ena amene adzanena kuti, "Nanga ngati ubatizo siupulumutsa, tibvutikiranji ndi kubatizidwa?" Ngakhale kuti ubatizo siupulumutsa, koma uli wofunika.



kuposa mau ena ali onse. Zocita zace zina zonse ziri gawo la nchito yace yaikuru imeneyi. Pa Yohane 16:14 tiwerenga mau a Yesu pamene ananena za kuti nchito ya Mzimu Woyera idzakhala ngati wa zinthu izo zimene anthu ambiri amanena kuti amacita ndi mphamvu ya Mzimu Woyera. Ngati Yesu salemekezedwa mwa Iwo, koma munthu, ndiye kuti sizinacitika mwa mphamvu ya Mzimu Woyera wa Mulungu.

Pamene tiri kuganizira za nchito ya Mzimu Woyera tifuna kuganizira za iwo pa mitu iwiri yosiyana: 1. Nchito ya Mzimu Woyera ndi mtima wace wa munthu wotaika ndipo, 2. Nchito ya Mzimu Woyera mu mtima mwa Mkristu.

**1. Nchito ya Mzimu Woyera mu mtima mwa munthu wosapulumuka.**

Pali mau amodzi amene amatiuza ife za nchito ya Mzimu Woyera mumtima mwa munthu wosapulumuka. *"Ndipo atadza Iyeyo, adzatsutsa dziko lapansi za macimo, ndi zacilungamo, ndi zaciweruzo; za macimo cifukwa sakhulupirira Ine, za cilungamo cifukwa ndinka kwa Atate, ndipo simundionanso; za ciweruzo cifukwa mkuru wa dziko ili lapansi waweruzidwa."* Yohane 16:8-11

Pamene munthu wosapulumutsidwa adziwa kuti ali wocimwa, ndi kuti Yesu ali wangwiro, ndipo kuti iye ayenera kukumana ndi Yesu pa ciweruzo cikubweraco cifukwa ca ucimo wace, ndi Mzimu Woyera amene ali kugwira nchito mu mtima mwace.

**2. Nchito ya Mzimu Woyera m'moyo wa Mkristu.**

Pali nchito zambiri zimene Mzimu Woyera amacita mumtima mwa Mkristu. M'phunziro ili tidzaganizira zinthu zisanu ndi ziwiri za nchito zimenezi.

(1) Mzimu Woyera ndiye wogawira moyo watsopano

*"Koma nati Mzimu wa Iye amene adaukitsa Yesu kwa akufa akhalabe mwa inu, Iye amene adaukitsa Kristu Yesu kwa akufa adzapatsanso moyo matupi anu akufa mwa Mzimu wace wakukhala mwa inu."* Aroma 8:11

(2) Mzimu Woyera ndiye msangalasi wathu

*"Ndipo Ine ndidzapempha Atate ndipo adzakupatsani inu Nkhoswe yina, kuti akhale ndi inu ku nthawi zonse."* Yohane 14:16

(3) Mzimu Woyera ndi mphunzitsi wathu

*"Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa, Iyeyo adzaphunzitsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu."* Yohane 14:26

(4) Mzimu Woyera atipanga ife kukhala azipatso m'moyo wa Cikristu

*"Koma cipatso ca Mzimu ndico cikondi, cimwemwe, mtendere, kuleza mtima, cifundo, kukoma mtima, cikhulupiriro, cifatso, ciletso."* Agalatiya 5:22-23a

(5) Mzimu Woyera amatipatsa mphamvu zogwirira nchito

*"Komatu mudzalandira mphamvu, mzimu woyera atadza pa inu: ndipo mudzakhala mboni zanga m'Yerusalemu, ndi m'Yudeya lonse, ndi m'Samariya, ndi kufikira malekezero ace a dziko."* Macitidwe 1:8

(6) Mzimu Woyera utilangiza pamene tigwira nchito ya Mulungu

*"Ndipo pa kutumikira Ambuye iwowa, ndikusala cakudya, Mzimu Woyera anati, Mundipatulire ine Barnaba ndi Saulo ku nchito imene ndinawaitanilako."* Macitidwe 13:2

*"Ndipo anapita padziko la Frugiya Galatiya, atawaletsa Mzimu Woyera kuti asalalikire mau mu Asiya."* Macitidwe 16:6

(7) Mzimu Woyera ndiye wopatsa mphatso za uzimu

*"Koma zonse izi acita Mzimu m'modzi yemweyo, nagwira yense pa yekha monga afuna."* 1 Akorinto 12:11

Izi ndizo zinthu zowerengeka zimene ziyenera kuzindikirika bwino-bwino ponena za "mphatso za uzimu." Zoonadi izi zidzaoneka pa kuphunzira mosamala mitu ya 12, 13, and 14 ya 1 Akorinto.

A. Mphatso za uzimu zigawidwa ndi Mzimu Woyera ndipo mphatso zosiyana-siyana zipatsidwa kwa anthu osiyana-siyana. Cifukwa kuti munthu wina salandira mphatso yofanana ndi imene alandira wina, ici sicitanthauza kuti Mkristu wina ali wotsika kusiyana ndi ena ai.

B. Mphatso zonse za Mzimu Woyera zidzakhala zobweretsa ulemerelo kwa Yesu Kristu, cifukwa iyi ndi nchito ya Mzimu Woyera zidzakhala zobweretsa ulemerelo kwa Yesu Kristu, cifukwa iyi ndi nchito ya Mzimu Woyera. Werenganinso Yohane 16:14a.



*"Ndipo tiganizirane wina ndi mnzace kuti tifulumizane ku cikondano ndi nchito zabwino, osaleka kusonkhana kwathu pamodzi, monga amacita ena, komatu tidandaulirane, ndiko koposa monga momwe muona tsiku liri kuyandikira."* Ahebri 10:24, 25

*"Cimene tidaciona, ndipo tidacimva, tikulalikirani inunso, kuti inunso mukayanjane ndi ife; ndipo ciyanjano cathu cirinso ndi Atate, ndipo ndi Mwana wace Yesu Kristu."* 1Yohane 1:3

**2. Nthawi zonse poyenera kuti pazikhala cifukwa ceni-ceni ndi makhalidwe pamene mpingo upereka cilangizo kwa munthu.**

*"Kuti mzimu upulumutsidwe m'tsiku la Ambuye Yesu."* 1 Akorinto 5:5b

Pamene pali poyenera kupereka langizo, ciyenera kuperekedwa ndi mpingo mwa cikondi. Sicifunika konse-konse kucitika ngati mobwezera zowawa kapena ngati cilango, koma ndi mtima wofuna kuti wocimwayo aone cimo lace, alape, ndi kubwerera kutsata Ambuye Yesu.

## NCHINTO YA MPINGO

**1. Kubweza wotaika kuti afike ku cikhulupiriro ca mwa Kristu kudzera mwa kulalikira uthenga wabwino.**

*"Cifukwa cace mukani, phunzitsani (pangani akuphunzira) anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana ndi la Mzimu Woyera."* Mateyu 28:19

*"Ndi kuti kulalikidwe m'dzina la kulapa ndi kukhululukidwa kwa macimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu."* Luka 24:47

*"Pakuti Uthenga Wabwino wa Kristu sundicititsa manyazi; pakuti uli mphamvu ya Mulungu yakupulumutsa munthu aliyense wakukhulupirira."* Aroma 1:16a

**2. Kubatiza iwo amene apulumutsidwa.**

*"Cifukwa cace mukani, phunzitsani (pangani akuphunzira) anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera."* Mateyu 28:19

*"Pamenepo iwo amene analandira mau ace anabatizidwa."* Macitidwe 2:41a

**3. Kuphunzitsa mokwanira bwino njira ya moyo wa Cikristu.**

*"Kuwaphunzitsa iwo, asunge zinthu zonse zimene ndinakulamulirani inu."* Mateyu 28:20a

*"Pakuti sindinakubisirani pakukulalikirani uphungu wonse wa Mulungu."* Macitidwe 20:27

**4. Kupembedza, kulimbikitsana wina ndi mnzace, ndi ciyanjano.**

*"Ndipo anali cikhalire m'ciphunzitso ca atumwi ndi m'ciyanjano, m'kunyema mkate ndi mapemphero."* Macitidwe 2:42



C. Mphatso ya malilime siikanidwa koma isungidwa ngati mphatso yosafunika kwambiri.

D. Mkristu aumurizidwa kuti afune mphatso zabwino kwambiri. Mphatso yoposa zonse ndiyo 'Cikondi.' (Onani 1 Akorinto 13:1-13). Inde ndi mphatso yolalikira. (Onani 1 Akorinto 14:1, 39).

E. Ngati munthu afuna kulankhula m'zilankhulidwe zina mu nyumba ya Mulungu, pali malamulo ace amene ayenera kutsatidwa:

Pasalankhule anthu oposa awiri kapena atatu. 1 Akorinto 14:27

Asalankhule pa nthawi imodzi onse koma m'modzi-m'modzi. 1 Akorinto 14:27

Asaloledwe kulankhula koma pokha-pokha pali munthu womasulira. 1 Akorinto 14:27b, 28

Zolankhulidwazo zikhale za ulemerelo wa kwa Yesu Kristu ndi zolimbitsa mpingo. Yohane 16: 14 ndi 1 Akorinto 14:26b.

## KUKHALA NDI MZIMU WOYERA

Buku Lopatulika litiphunzitsa kuti Mzimu Woyera ukhala mu mtima mwa Mkristu aliyense. Pamene munthu wabadwanso kwatsopano, Mzimu wa Mulungu ulowa mumtima mwace, iye sali Mkristu.

*"Tsopano ngati munthu alibe Mzimu wa Kristu, licitike mwa a mitundu; kuti tikalandire lonjezano la Mzimu Woyera mwa cikhulupiriro."* Agalatiya 3:14

## KUDZAZIDWA NDI MZIMU WOYERA

Pali kusiyana kwakukuru pakati pa Mzimu Woyera kukhala mu mtima mwa munthu ndi Mzimu Woyera kudzaza mumtima mwa Mkristu. Mulungu afuna kuti mitima yathu iperekedwe kwa Iye kuti Mzimu Woyera wace udzaze ndi kutengeratu mitima yathu. Ndi nthawi imeneyi ndipo ndi nthawi yokhayo imene Mulungu angatigwiritse nchito m'njira yoyenera kutumikira Ambuye ndi Mpulumutsi wathu, Yesu Kristu.

*"Ndipo musaledzere naye vinyo, m'mene muli citaiko; komatu mudzale naye Mzimu."* Aefeso 5:18

***"Ndipo m'mene adapemphera iwo, padagwedezeka pamalo pamene adasonkhanirapo; ndipo anadzazidwa onse ndi Mzimu Woyera, nalankhula Mau a Mulungu molimbika mtima."***
**Macitidwe 4:31**

**Mulungu ali okonzeka ndi wankhawa kuti adzaze mtima uli onse ndi Mzimu wace. Komabe, ici cisanacitike, tiyambe tacotsa mumtima mwathu zinthu zonse zimene sizikondweretsa Mulungu. Payenera kukhala kukonzekera kumvera utsogoleri wa Mzimu Woyera m'zinthu zonse. Pamene takonzekera motero, tidzaona kuti Mzimu Woyera wadzazadi m'mitima yathu mwa njira yosadziwika.**



*"Pamenepo cinakomera atumwi ndi akuru ndi Eklesia yense kusankha anthu a m'guru lao, ndi kuwatumiza ku Antiokeya ndi Paulo ndi Barnaba."* Macitidwe 15:22a

Pamene mlandu unacitika woyenera kupatsidwa nao cilango ku mpingo, unali mpingo umene unali kuyenera kulangiza ndi kucitapo kanthu pa munthu wocimwayo. Onani 1 Akorinto 5:1-5

## AZITSOGOLERI A MPINGO

**1. Mbusa.**

Mau oti mbusa, mkuru ndi oyang'anira mpingo agwiritsidwa nchito mosinthika-sinthika m'Cipangano Catsopano. Pa Macitidwe mutu 20, Paulo anaitana akuru a mpingo ku Efeso (ndime 17). Mu ndime 28, iye awauza kuti Mzimu Woyera anawapanga iwo kukhala oyang'anira, ndi kuti iwo ayenera kudyetsa (mbusa) mpingo. Paulo alankhula za iye mwini monga mkuru mu 1 Petro 5:1.

Kapena funso lidzabwerapo, "Ndani ayenera kukhala mbusa wa mpingo?" Tipeza zoyenera za munthu kukhala mbusa zoperekedwa ndi Mulungu mu 1 Timoteo 3:1-7 ndi 1:7-9. Ndimo m'mene zimenezi ziyenera kuphunzitsidwira bwino-bwino ndi aliyense mu mpingo. Mpingo uyenera kukumbukanso kuti Mulungu anali ndi cifukwa pamene mpingo ufuna mbusa, uyenera kuonetsetsa kuti munthu ameneyo ali nazo zinthu zomuyenerazi asanaitanidwe kuti akhale mbusa wa mpingo.

**2. Atumiki.**

Mipingo ya Cipangano Catsopano inalinso ndi atumiki. Zoyenera makhalidwe a atumiki zipezeka mu 1 Timoteo 3:8-13

## KUDZISUNGIRA ULEMU KWA MPINGO

**1. Pali nthawi pamene cilango cifunika.**

Pamene moyo wa munthu wa mu mpingo ucita zinthu zosiyana ndi ziphunzitso za Yesu kuti alikudzetsa manyazi ku mpingo ndi kuononga za Kristu, cimakhala cofunika ku mpingo kuti amulangize iye.

*"Kumpereka iye wocita cotere kwa Satana, kuti liononongeke thupi."* 1 Akorinto 5:5a

**wolembedwa kuti: Malamulo a mpingo a zokambirana pa ubatizo wa Mau a Mulungu.)**

*"Cifukwa cace mukani, phunzitsani anthu a mitundu yonse, ndi kuwabatiza iwo m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera."* Mateyu 28:18

*"Pamenepo iwo amene analandira mau ace anabatizidwa, ndipo anaonjezedwa tsiku lomwelo anthu ngati zikwi zitatu."* Macitidwe 3:41.

Kucokera pa ndime izi ndi zina zambiri, tiphunzirapo kuti Yesu analamulira ubatizo, ndipo kuti mipingo ya Cipangono ca Tsopano inacita ubatizo. Ndico cifukwa cace tinena kuti a mumpingo a Cipangano ca Tsopano alandire ubatizo wa Cipangano ca Tsopano.

## ULAMULIRO WA MPINGO

Mipingo yomwe imatsatira ciphunzitso ca Cipangano Catsopano ikhulupirira mwa kucita ulamuliro wa mpingo mwa ufulu. Cikhulupiriro ici ndi kucita kumeneku zicitika cifukwa ca zinthu izi:

**1. Ukuru wa Yesu Kristu.**

Taona poyamba pa mutu uwu kuti Kristu ndiye mutu wa mpingo. Iye ku mpingo ali cimodzi-modzi monga uli mutu ku thupi. Ndi mutu umene ulamulira ciwalo ciri conse ca thupi. Monga momwemo, ndi Kristu kudzera mwa Mzimu Woyera, amene atsogolera Mkristu aliyense ndi kulamulira thupi lonse.

**2. Kufanana kwa okhulupirira onse**

Buku Lopatulika liphunzitsa kuti ife tonse ndife ziwalo za thupi. Palibe ciwalo cina ca thupi cimene cingalamulire ciwalo cinzace ca thupi. Dzanja silingauze mwendo coyenera kucita...iyi ndi nchito ya mutu. Phunzirani bwino-bwino. Aroma 12:3-6 ndi 1 Akorinto 12:14-20

**3. Zitsanzo zooneka mu Cipangano Catsopano.**

Pamene atumiki anayenera kusakhidwa, cinali kucitika ndi mpingo womwewo. Werengani mu Macitidwe 6:1-6

Pamene Akristuwo anali ndi cobvuta cacikuru, unali mpingo wa komweko umene unali kuganizira cocita.





## CIMO NDI SATANA

Pali mafunso ambiri ofunsa za Satana amene sangatheke kuyankhidwa cifukwa Mulungu sanasankhe kutiuza ife m'Buku Lopatulika. Kamabe, zokwanira zinaululidwa kuyankha mafunso ena apafupi. Buku Lopatulika litiphunzitsa zokwanira kuti tingathe kuzindikira bwino-bwino za makhalidwe ace a mdani wathu wa zauzimu, Satana. Tsopano tiyeni tiganizire mafunso ena amene anafunsidwa nthawi zambiri onena za Satana.

**1. Kodi Satana anacokera kuti?**

Buku Lopatulika litiphunzitsa bwino-bwino kuti Mulungu analenga zinthu zonse. Popeza mau amenewa ngoonadi, ncoonekeratu kuti Satana ayenera kukhala atalengedwa ndi Mulungu.

**2. Kodi Mulungu analenga Satana kuti akhale oipa monga aliri tsopano lino?**

Yankho ndilo, AI. Mulungu nthawi zonse amacita monga mwa makhalidwe ace. Ndi cinthu cotsutsana ndi makhalidwe a Mulungu kulenga cinthu cimene ciri coipa. Tiyeni tiyang'ane ku dziko lathu lapansi mwa citsanzo. Pali zoipa zambiri pa dziko lapansi lero. Sizinali zotere pamene Mulungu analenga dziko lapansi poyamba paja. *"Ndipo anaziona Mulungu zonse zimene adazipanga, ndipo, taonani, zinali zabwino ndithu."* Genesis 1:31a. Tizindikira nthawi yomwe ino kuti dziko lapansi siliri monga momwe analilengera Mulungu...cosintha cabwerapo. Ndi monga momwemo ndi Satana. Tsopano iye ali mdierekezi, ngakhale kuti Mulungu sanamulenge wotero. Pamene tiphunzira Cipangano ca Tsopano, kuoneka ngati kuti Satana anali mngelo amene anacimwa kwa Mulungu ndipo anaponyedwa pansi kucokera kumwamba. Werengani Mau a Mulungu awa bwino-bwino:

*"Pakuti ngati Mulungu sadalekerera angelo adacimwawo, koma anawaponya ku ndende nawaika ku maenje a mdima, asungike akaweruzidwe."* 2 Petro 2:4

*"Angelonso amene sanasunga cikhalidwe cao coyamba komatu anasiya pokhala pao-pao, adawasunga m'ndende zosatha pansi pa mdima, kufikira cimaliziro ca tsiku lalikuru."* Yuda 1:6

*"Ndipo anati kwa iwo, Ndinaona Satana alinkugwa ngati mphezi wocokera kumwamba."* Luka 10:18

**3. Kodi nchito ya Satani nciani?**

Dzina lace lomwelo litanthauza kuti iye ndiye mdierekezi. Iye atsutsana ndi Mulungu ndi onse amene atsata Mulungu. Iye amayesa, amanyenga, ndipo amafuna kukoka ena kuti apite ku gahena pamodzi ndi iye.

**4. Cimariziro cace cidzakhala cotani?**

Cilango cosatha m'gahena ndico cidzakhala cimariziro cace ca Satana ndi ca onse om'tsata iye.

*"Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya moto ndi Sulfure."* Cibvumbulutso 20:10a

*"Pomwepo Iye adzanena kwa iwo a ku dzanja la manzere, Cokani kwa Ine otembereledwa inu, ku Moto wa nthawi zonse wokorezedwera mdierekezi ndi amithenga ace."* Mateyu 25:41

## CIYAMBI CA CIMO

Tisanayambe kuphunzira za ciyambi ca cimo, tiyenera kupeza yankho limene limveka kawiri-kawiri. Cifukwa ciani Mulungu wa mphamvu zonse amene siafuna cimo analora cimo kubwera ku dziko lapansi? Yankho ndi lapafupi. Ngati Mulungu akanalenga munthu amene akanapereka cikondi cacikuru ndi coonadi nakhala omvera, munthuyo akanakhala ndi mphamvu yodana ndi Mulungu ndi kusamvera Mulungu. Taganizirani cimeneci mwa njira iyi. Tiyeni tinene kuti inu muli ndi ana amuna awiri amene muwakonda kwambiri. Inu mufuna kuti ana amenewa akukondeni ndi kukumverani. Ndiye kapena tsiku lina kunali kofunika kuti inu mupite pa ulendo. Ulendowo ukanakhala wa tsiku lathunthu. Inu munadziwa kuti cidzakhala coopsa kwa anawo kusewera ku thengo. Cifukwa cace munawaitana iwo ndipo munati, "Ndiyenera kucokapo tsiku lonse. Khalani poyera pafupi ndi nyumba ino. Musasewere ku thengo." Pamene munamangirira m'modzi wa anawo ku mtengo wa pakhomopo. Panalibe njira ina yoti akanatha kucokapo ndi kukasewera ku thengo. Mwana waciwiriyo anapatsidwa ufulu wakuyenda-yenda monga m'mene akanafunira.

Tsopano ana onsewa analamulidwa kuti akhale pa nyumbapo. M'modziyo sakanatha kukhala osamvera, winayo akanakhala osamvera. Pamene munabwerera pa madzulo atsikulo, munamva kuti ana onsewa anali pakhomo pomwepo sanacokepo. Zoonadi m'modziyo sakanatha kukhala osamvera cifukwa anali omangidwa ku mtengo. Winayo anaonetsa cikondi cace ndi



Pa mutu uwu, pamene tirikuphunzira za mpingo, tidzakhala tiri kuganizira za msonkhano wa guru wamba, looneka ndi maso, ndi guru lopangana mogwirizana. Tidzafuna kuonetsetsa kuti makhalidwe a mipingo iyi ya Cipangano ca Tsopano adzakhalanso makhalidwe a mpingo wathu.

## MUTU WA MPINGO

Palibe munthu kapena guru la anthu limene lingathe kukhala mutu wa mpingo wa Cipangano ca Tsopano. Yesu yekha ndiye mutu wa mpingo. Yense amene afuna kutenga malo a ukuru mu mpingo ameneyo alikufuna kutenga malo amene pa cilungamo ali a Yesu Kristu.

"Ndipo anaika zonse pansi pa mapazi ace, nampatsa Iye akhale mutu pamwamba pa zonse za Eklesia."

Ndife ziwalo za mpingo monganso ziri ziwalo zambiri za thupi limodzi. Yesu Kristu ndiye mutu wa mpingo.

## KUKHALA CIWALO CA MPINGO

Mu Cipangano ca Tsopano tipeza kuti pali mapangano awiri opatsidwa cifukwa ca kukhala ciwalo ca mu mpingo:

Cipulumutso ndi ubatizo.

**1. Mpingo uyenera kukhala ndi anthu opulumuka kuti akhale ziwalo za mu mpingo.**

*"Ndipo Ambuye anawaonjezera tsiku ndi tsiku amene akuti apulumutsidwe."* Macitidwe 2:47b

*"Kwa mpingo wa Mulungu wa kukhala m'Korinto, ndiwo oyeretsedwa mwa Kristu Yesu."* 1 Akorinto 1:2a

Ndi zoonadi kuti nthawi zina anthu amene asanapulumuke asanduka ziwalo za mpingo. Munthu ali wotero. Ndiko kutsutsana ndi cikonzedwe ca Mulungu. Anthu ena asanduka a mu mpingo kudzera ma kubvomereza mwa cikhulupiriro conama. Anthu ena amadza ndi tiana kukhala ziwalo za mpingo. Mulungu afuna iwo okha amene anabadwanso kwa tsopano kukhala ziwalo za mu mpingo.

**2. Mpingo uyenera kukhala ndi okhawo amene ali obatizidwa mwa mau a Mulungu kukhala ziwalo zace. (Onani mutu**

## MPINGO (Eklesia)

Pamene womanga ali kumanga nyumba, ayenera kutsata cikonzedwe cacithunzi ca nyumba cimene cajambulidwa. Mulungu anapereka kwa ife cithunzi cacikonzedwe ca mpingo m'Cipangano ca Tsopano. Tiyenera kutsata cikonzedwe caceco mosamala bwino ngati tiyenera kumanga mipingo imene idzakhala yokondweretsa kwa Mulungu.

Mau oti 'mpingo' agwiritsidwa nchito nthawi zokwanira zana limodzi kudza khumi limodzi ndi mphambu zinai (114) m'Cipangano ca Tsopano. Pafupi-fupi m'njira ili yonse mauwa anena za guru la Akristu okhala pamodzi ndi kupembedza pamodzi pa malo ena. Komabe, mauwa pa nthawi zina zocepa anagwiritsidwa nchito pa kutanthauza anthu onse okhulupirira, obadwanso kaciwiri okhala pa guru limodzi. Ponena mwa tanthauzo ili, liphunzitsa coonadi kuti akukhulupirira obadwanso kaciwiri ali ogwirizana pamodzi mwa uzimu ndi Kristu monga momwe ziwalo zathupi zonse zigwirizana ndi mutu. Pamene mau onena kuti 'mpingo' agwiritsidwa nchito mwa njira iyi, kawiri-kawiri timatanthauza 'Mpingo wa ponse-ponse' kapena 'Mpingo wosaoneka ndi maso.' Mu Mau a Mulungu ali pansiwa, tingathe kuwagwiritsa nchito mwa njira imeneyi.

*"Pakuti mwamuna ndiye mutu wa mkazi, monganso Kristu ndiye mutu wa Eklesia, ali yekha Mpulumutsi wa thupilo."* Aefeso 5:23

*"Ndipo Iye ali mutu wa thupi, Eklesiayo."* Akolose 1:18

Pophunzira mosamala Mau a Mulungu tidzaonetsetsa kuti pa mau onse onena kuti 'Eklesia' (mpingo) atanthauza guru lapadera la a Kristu.

*"Ndipo kunali aneneri ndi aphunzitsi ku Antiokeya mu mpingo wakomweko."* Macitidwe 13:1a

*"Ndipo pokhala ku Mileto anatuma ku Efeso, naitana akuru a mpingo."* Macitidwe 20:17

*"Ndipo mulankhule Mpingo wa Ambuye wa m'nyumba."* Aroma 16:5a

*"Cimene upenya, lemba m'buku, nulitumize ku Mipingo isanu ndi iwiri, imene ili mu Azia."* Cibvumbulutso 1:11b



kumvera kwace pamene anakhala pa nyumbapo nthawi zonse ngakhale kuti anali ndi ufulu wocokapo. Pomwepo tikadanena kuti mwana amene akanakhala osamvera koma anasankha kumvera anaoneka kumvera kwakukuru kwa inu.

Mulungu sanapereka mwai wa cimo m'munda muja ndipo anapatsa munthu mphamvu yakusankha kotero kuti sakanamvera. Mulungu anacita ici kuti munthu aonetse cikondi cace cacikuru kwa Mulungu ndiponso kuti aonetse kumvera kwakuru. Pamene munthu anasankha kusamvera, cimo linalowa pa dziko lapansi.

Werengani bwino-bwino Genesis 2:8 kufika Genesis 3:24. Ndime imeneyi, imene ikamba za cimo loyamba, itithandiza ife kuzindikira zinthu zambiri za cimo. Tiphunzira zoonadi izi kucokera pa ucimo:

1. Mulungu anapereka zonse zimene zinali zabwino kwa munthu.
2. Mulungu anakaniza zokha zimene zinali zoipa kwa munthu.
3. Satana, mooneka ngati njoka, anabwera namuyesa Hava. Iye anayesa kumuuza Hava kuti Mulungu anali kumubisira cinthu cina cabwino. Anamuuzitsa Hava kuti Mulungu sakanamulanga ndi imfa ngati akanakhala osamvera.
4. Hava anasankha kukhala osamvera cifuniro ca Mulungu ndipo anadya cipatso coletsedwaco. Ndipo anapereka kwa Adamu nayenso anadyako.

### KUFOTOKOZERA CIMO

Kucokera pa zinthu tanena pamwambazi, tifuna kudziwa bwino za kuti cimo ndi ciani. **Cimo ndilo kukana cifuniro ca Mulungu ndi kuti munthu acite cifuniro ca iye mwini.** Ici ndi ceni-ceni cimene anacita Adamu ndi Hava. Anacidziwa cifuniro ca Mulungu koma anasankha kukana cifuniro ca Mulunguco kuti iwo akanakhoza kucita cinthu cimene akanafuna kucita.

### CIMO LIRI KWA ANTHU ONSE PONSE-PONSE

Mulungu atiphunzitsa ife m'mau ace kuti anthu onse kuli konse anacimwa kwa Iye. Pa maweruzidwe a munthu, tingathe kukhala ngati abwino kwambiri. Koma Mulungu waweruza monga m'mene aweruzira munthu. Mulungu atifanizira ife ndi cilungamo cace ca Iye mwini. Pamene Mulungu wacita ici, anena kuti onse anacimwa.

*"Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerelo wa Mulungu."* Aroma 3:23

*"Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha."* Yesaya 53:6

*"Tikati kuti tilibe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi."* 1 Yohane 1:8

*"Potero kwa iye amene wodziwa kucita bwino, koma sacita, kwa iye kuli cimo."* Yakobo 4.17

## ZOTSATIRA ZACE ZA UCIMO

Ncosatheka kulemba mndandanda wa zoipa zonse zimene zabwera pa dziko lapansi cifukwa ca ucimo. Mau sangathe kukamba za cisoni ndi zowawa zimene zinabwera ndi cimo. Pamene tiyang'anitsitsa pa dziko lapansi lero ndi zowawa njara, ndi umphawi, tiyenera kukumbukira kuti Mulungu sanalenga dziko lotere. Dziko silinali lotere mpaka nthawi imene cimo linalowa pa dziko. Makamaka tifuna kulozapo njira ziwiri zimene cimo linaipitsira munthu.

**1. Cimo liononga ciyanjano cathu ndi Mulungu.**

Pamene cimo linalowa mumtima mwa Adamu ndi Hava, anadziwa kuti anacimwa. Anafuna kubisa umalisece wao ndi kubisala Mulungu. Cimo lao linawacotsetsa m'munda uja wa Edeni ndiponso pamaso pa Mulungu. Tsopano, monga momwemo, cimo lisiyanitsa ndi Mulungu.

*"Koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu, ndipo macimo anu abisa nkhope yace kwa inu, kuti Iye sakumva."* Yesaya 59:2

**2. Ucimo ubweretsa cilango cosatha; m'gahena.**

*"Pakuti mphoto yace ya ucimo ndi imfa."* Aroma 6:23a

*"Ndipo imfa ndi Hade zinaponyedwa m'nyanja ya moto. Iyo ndiyo imfa yaciwiri. Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'buku la moyo anaponyedwa m'yanja ya moto."* Cibvumbulutso 20:14, 15

*"Koma amantha, ndi osakhulupirira, ndi onyansa, ndi acigololo, ndi olambira mafano, ndi onse amabodza, colandira cao cidzakhala m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure ndiyo imfa yaciwiri."* Cibvumbulutso 21:8



**2. Okhulupirirayo asanduka wolengedwa watsopano ndi Mzimu wa Mulungu wokhala mwa iye. Tsopano iye afuna kucita cifuniro ca Mulungu.**

*"Cifukwa cace ngati munthu aliyense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano."* 2 Akorinto 5:17

*"Tsopano ngati munthu alibe Mzimu wa Kristu, siali wace wa Kristu."* Aroma 8:9b

**3. Wokhulupirirayo, cifukwa cokhala ndi Mzimu wa Mulungu, adzatumikira Mulungu osatumikira Satana.**

*"Ndi kuti munatembenukira kwa Mulungu posiyana nao mafano, kutumikira Mulungu weni-weni wamoyo."* 1 Atesalonika 1:9b

*"Pakuti ife ndife a nchito anzace a Mulungu."* 1 Akorinto 3:9a

**4. Wokhulupirira ali ndi mudzi wosatha m'mwamba ulikudikira iye.**

*"M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ndipo ngati sikudali kotero, ndikadakuuzani inu. Ine ndipita kukakukonzerani inu malo."* Yohane 14:2

*"Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka: pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse."* 1 Atesalonika 4:16, 17.

**5. Wokhulupirirayo asungidwa ndi mphamvu ya Mulungu kotero kuti pamene wapulumutsidwa sadzatayikanso.**

*"Amene musungidwa ndi mphamvu ya Mulungu mwa cikhulupiriro, kufikira cipulumutso cokonzeka kukabvumbulutsidwa nthawi yotsiliza."* 1 Petro 1:5.

*"Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine; Ndipo Ine ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sizidzaonongeka ku nthawi zonse, ndipo palibe munthu adzazikwatula m'dzanja langa."* Yohane 10:27, 28

Mulungu momveka bwino atiphunzitsa ife m'mau ace kuti munthu ayenera kulapa asanalandire cipulumutso.

*"Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kulalikira, ndi kunena, Tembenukani mitima, pakuti ufumu wa kumwamba wayandikira."* Mateyu 4:17

*"Ndinena kwa inu , Iaitu; koma ngati inu simutembenuka mtima mudzaonongeka nonse momwemo."* Luka 13:3

*"Ndi kucitira umboni Ayuda ndi Ahelene wa kutembenuza mtima kulinga kwa Mulungu, ndi cikhulupiriro colinga kwa Ambuye wathu Yesu Kristu."* Macitidwe 20:21

Cikhulupiriro ndi cikakamizo cimene ciutsa cikhulupiriro pa moyo ku cinthu cimene ucikhulupiriraco. Cikhulupiriro ca mwa Yesu Kristu ndico cikhulupiriro cimene ciutsa munthu kuti moyo wace ukhulupirire pa Yesu. Cipulumutso cilandiridwa pamene cikhulupiriro coteroco caikidwa mwa Iye monga Mpulumutsi ndi Ambuye.

*"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha."* Yohane 3:16

*"Ndipo iwo anati, Ukhulupirire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi a pa banja ako."* Macitidwe 16:31

*"Popeza tsono tayesedwa wolungama ndi cikhulupiriro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Kristu."* Aroma 5:1

*"Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu." Aefeso 2:8*

## ZOTSATIRA ZACE ZA CIPULUMUTSO

**1. Okhulupirirayo ayeretsedwa ndi kukhululukidwa macimo ace onse.**

*"Tiyeni, tsono, tiweruzane, ati Yehova; ngakhale zoipa zanu ziri zofiira, zidzayera ngati matalala; ngakhale ziri zofiira ngati kapezi, zidzakhala ngati ubweya wa nkhosa, woti mbu."* Yesaya 1:18

*"Kuti ndidzacitire cifundo zosalungama zao, ndipo zoipa zao sindidzazikumbukanso."* Ahebri 8:12

*"Kwa Iye amene anatikonda ife, natimasula ku macimo athu ndi mwazi wace."* Cibvumbulutso 1:5b



*"Pomwepo Iye adzanena kwa iwo a ku dzanja lamanzere, cokani kwa Ine otembereredwa inu, ku moto wa nthawi zonse wokolezedwera mdierekezi ndi amithenga ace."* Mateyu 25:41

Munthu angathe kunyozera kapena kuliseka cimo, koma Mulungu satero. Mulungu aona cimo ndi kulanga cimolo. Tsopano tonsefe tinacimwa ndipo palibe cina cimene tingacite kuti tithawe cilango cimene tiyenera kulandira. Koma Mulungu, m'cikondi cace ca pa ife, anapanga njira yakuti cimo lathu lilangidwe ndipo ife tipulumuke. Phunzirani bwino mutu wa patsogolowu za Cipulumutso.

## CIPULUMUTSO

Pa phunziro lathali tinaphunzira kuti anthu onse anacimwa ndipo ali pansi pa ciweruzo ca Mulungu. Pa mutu uwu tifuna kuti tiphunzire za njira ya cipulumutso imene Mulungu anapereka mwaulere kwa anthu onse kudera mwa Mwana wace, Yesu Kristu. Cinthu coyamba cimene tiyenera kuzindikira ndi ici:

### MUNTHU SANGATHE KUDZIPULUMUTSA YEKHA

Tiyeni tiganizire zifukwa zinai za kuti munthu sangathe kudzipulumutsa yekha:

**1. Munthu sangathe kudzipulumutsa yekha cifukwa cilungamo ceni-ceni cimene iye angathe kuonetsa ciri coperewera kutali ndi cilungamo cimene ciri cokondweretsa pamaso pa Mulungu.**

*"Pakuti tonse takhala ngati cinthu cosakonzeka, ndi zolungama zathu zonse ziri ngati cobvala codetsedwa."* Yesaya 64:6a

**2. Munthu sangathe kudzipulumutsa yekha cifukwa Mulungu atiuziratu kuti palibe munthu adzapulumuka cifukwa ca nchito zace.**

*"Pakuti muli wopulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiriro, ndipo ici cosacokera kwa inu; ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera ku nchito, kuti asadzitamandire munthu aliyense."* Aefeso 2:8, 9.

3. Munthu sangathe kudzipulumutsa yekha cifukwa ayenera kulandira mphotho ya macimo ace...imfa.

*"Pakuti mphotho yace ya ucimo ndi imfa."* Aroma 6:23a

4. Munthu sangadzipulumutse yekha cifukwa munthu wocimwa ali wakufa kale mu uzimu. Tiwerenga Buku Lopatulika kuti munthu asanalandire moyo watsopano kudzera mwa Yesu Kristu, ali wakufa m' zolakwa ndi macimo.

*"Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zocimwa zanu."* Aefeso 2:1

Monga momwe amakhalira munthu wakufa m' moyo wathupi kuti sangathe kucita kathu, momwemonso, munthu wakufa mwa uzimu sangathe kucita kanthu kakudzipatsa yekha moyo wa uzimu.



### MULUNGU ANAPEREKA NJIRA YA CIPULUMUTSO CA MUNTHU

**1. Njira ya cipulumutso iyi ndiye Yesu.**

Pali anthu ambiri amene amadziwa kuti sangathe kudzipulumutsa okha ndi kuti ayenera kupeza thandizo. Komatu amalakwa pa kuyang'ana ku cinthu ca cabe kuti apeze thandizo. Ena akhulupirira mu ubatizo wao. Ena akhulupirira pa kukhala ciwalo cimodzi ca mu mpingo wao. Ena akhulupirira mu ufiti ndi m' mafano. Mulungu anapereka njira imodzi ya cipulumutso ya kwa anthu onse a pa dziko lapansi ndipo njira iyi ili mwa Yesu Kristu. Yesu ndipo Yesu yekhayo angathe kutipulumutsa ife ku macimo athu ndi ku cilango cosatha ca ku gahena.

*"Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo: Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine."* Yohane 14:6

*"Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo."* Macitidwe 4:12

**2. Njira ya cipulumutso iyi ikhala yotheka kudzera mwa imfa ya Yesu ya pa mtanda yofera ocimwa onse.**

*"Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse."* Yesaya 53:6

*"Monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri kucotsa macimo."* Mateyu 26:28

*"Ameneyo sanadziwa ucimo anamyesera ucimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa Iye."* 1 Akorinto 5:21

*"Amene anasenza macimo athu mwini yekha m'thupi mwace pa mtanda, kuti ife, titafa ku macimo tikakhale ndi moyo kutsata cilungamo; ameneyo mikwingwirima yace munaciritsidwa nayo."* 1 Petro 2:24

### CIPULUMUTSO CILANDIRIDWA PA KULAPA NDI KUKHULUPIRIRA

Kulapa ndiko kusinthika kwa mtima kumene zotsatira zace zionekera pa kusinthika kwa macitidwe a zocita. Kulapa kweni-kweni kukhudza zinthu zitatu; pa kudziwa kuti unacimwa kwa Mulungu; pa kumva cisoni cifukwa ca ucimo; pa kuleka cimo.

## MUTU 7

### MPINGO (Eklesia)

Pamene womanga ali kumanga nyumba, ayenera kutsata cikonzedwe cacithunzi ca nyumba cimene cajembulidwa. Mulungu anapereka kwa ife cithunzi cacikonzedwe ca mpingo m'Cipangano ca Tsopano. Tiyenera kutsata cikonzedwe caceco mosamala bwino ngati tiyenera kumanga mipingo imene idzakhala yokondweretsa kwa Mulungu.

Mau oti 'mpingo' agwiritsidwa nchito nthawi zokwanira zana limodzi kudza khumi limodzi ndi mphambu zinai (114) m'Cipangano ca Tsopano. Pafupifupi m'njira ili yonse mauwa anena za gulu la a kristu okhala pamodzi ndi kupembedza pamodzi pa malo pena. Komabe, mauwa pa nthawi zina zocepa anagwiritsidwa nchito pakutanthauza anthu onse okhulupilira, obadwanso kaciwiri okhala pagulu limodzi. Ponena mwa tanthauzo ili, liphunzitsa coonadi kuti akukhulupilira obadwanso kaciwiri ali ogwirizana pamodzi mwa uzimu ndi Kristu monga momwe ziwalo zathupi zonse zigwirizana ndi mutu. Pamene mau onena kuti 'mpingo' agwiritsidwa nchito mwa njira iyi, kawiri kawiri timatanthauza 'Mpingo wa ponse ponse' kapena' Mpingo wosaoneka ndi maso.' M'mau a Mulungu ali pansiwa, tingathe kuwagwiritsa nchito mwa njira imeneyi.

Pakuti mwamuna ndiye mutu wa mkazi, monganso Kristu ndiye mutu wa Eklesia, ali yekha Mpulumutsi wa thupilo." Aefeso 5: 23.

"Ndipo Iye ali mutu wa thupi, Eklesiayo."
Akolose 1: 18.

Pophunzira mosamala mau a Mulungu tidzaonetsetsa kuti pa mau onse onena kuti 'Eklesia' (mpingo) atanthauza gulu lapadera la a kristu.

"Ndipo kunali aneneri ndi aphunzitsi ku Antiokeya mu mpingo wakomweko." Macitidwe 13: 1a.



cokera kumwamba. Welengani mau a Mulungu awa bwino-bwino:

"Pakuti ngati Mulungu sadalekelera angelo adacimwawo, koma anawaponya ku ndende nawaika ku maenje a mdima, asungike akaweruzidwe."
2 Petro 2: 4.

"Angelonso amene sanasunga cikhalidwe cao coyamba komatu anasiya pokhala pao pao, adawasunga m'ndende zosatha pansi pa mdima, kufikira cimalizilo ca tsiku lalikuru." Yuda 1: 6.

"Ndipo anati kwa iwo, Ndinaona Satana alinkugwa ngati mphezi wocokera kumwamba." Luka 10: 18.

3. Kodi nchito ya Satana nciani?

Dzina lace lomwelo litanthauza kuti iye ndiye mdierekezi. Iye atsutsana ndi Mulungu ndi onse amene atsata Mulungu. Iye amayesa, amanyenga, ndipo amafuna kukoka ena kuti apite ku gahena pamodzi ndi iye.

4. Cimariziro cace cidzakhala cotani?

Cilango cosatha m'gahena ndico cidzakhala cimariziro cace ca Satana ndi ca onse om'tsata iye.

"Ndipo mdierekezi wakuwasokeretsa anaponyedwa m'nyanja ya moto ndi Sulfure." Cibvumvulutso 20:10a.

"Pomwepo Iye adzanena kwa iwo a ku dzanja la manzere, Cokani kwa Ine otembereledwa inu, ku moto wa nthawi zonse wokorezedwera mdierekezi ndi amithenga ace." Mateyu 25: 41.

### CIYAMBI CA CHIMO

Tisanayambe kuphunzira za ciyambi ca chimo, tiyenera kupeza yankho limene limveka kawiri-kawiri. Cifukwa

ciani Mulungu wa mphamvu zonse amene siafuna chimo analora chimo kubwera ku dziko lapansi? Yankho ndi lapafupi. Ngati Mulungu akanalenga munthu amene akanapereka cikondi cacikuru ndi coonadi nakhala omvera, munthuyo akanakhala ndi mphamvu yodana ndi Mulungu ndi kusamvera Mulungu. Taganizirani cimeneci mwa njira iyi. Tiyeni tinene kuti inu muli ndi ana amuna awiri amene muwakonda kwambiri. Inu mufuna kuti ana amenewa akukondeni ndi kukumverani. Ndiye kapena tsiku lina kunali kofunika kuti inu mupite pa ulendo. Ulendowo ukanakhala wa tsiku la thunthu. Inu mudadziwa kuti cidzakhala coopsa kwa anawo kusewera ku thengo. Cifukwa cace munawaitana iwo ndipo munati, "Ndiyenera kucokapo tsiku lonse. Khalani poyera pafupi ndi nyumba ino. Musasewere ku thengo." Pamenepo munamangirira mmodzi wa anawo ku mtengo wa pakhomopo. Panalibe njira ina yoti akanatha kucokapo ndi kukasewera ku thengo. Mwana waciwiriyo anapatsidwa ufulu wakuyendayenda monga mmene akanafunira.

Tsopano ana onsewa analamulidwa kuti akhale pa nyumbapo. Mmodziyo sakanatha kukhala osamvera, winayo akanakhala osamvera. Pamene munabwerera pa madzulo a tsikulo, munamva kuti ana onsewo anali pakhomo pomwepo sanacokepo. Zoonadi mmodziyo sakanatha kukhala osamvera cifukwa anali omangidwa ku mtengo. Winayo anaonetsa cikondi cace ndi kumvera kwace pamene anakhala pa nyumbapo nthawi zonse ngakhale kuti anali ndi ufulu wocokapo. Pomwepo tikadanena kuti mwana amene akadakhala osamvera koma anasankha kumvera anaoneka kumvera kwakukuru kwa inu.

Mulungu sanapereka mwai wa chimo m'munda muja ndipo anapatsa munthu mphamvu yakusankha kotero kuti sakanamvera. Mulungu anacita ici kuti munthu aonetse cikondi cace cacikuru kwa Mulungu ndiponso kuti aonetse kumvera kwakuru. Pamene munthu anasankha kusamvera, chimo linalowa padziko lapansi.

Welengani bwino-bwino Genesis 2: 8 mpaka Genesis 3: 24. Ndime imeneyi, imene ikamba za chimo loyamba, itithandiza ife kuzindikira zinthu zambiri za chimo. Tiphunzira zoonadi izi kucokera pa ucimo:



5. <u>Wokhulupilirayo asungidwa ndi mphamvu ya Mulungu kotero kuti pamene wapulumutsidwa sadzatayikanso</u>.

"Amene musungidwa ndi mphamvu ya Mulungu mwa cikhulupiliro, kufikira cipulumutso cokonzeka kukabvumbulutsidwa nthawi yotsiliza,"1 Petro 1:5.

"Nkhosa zanga zimva mau anga, ndipo Ine ndizizindikira, ndipo zinditsata Ine; Ndipo Ine ndizipatsa moyo wosatha; ndipo sizidzaonongeka ku nthawi zonse, ndipo palibe munthu adzazikwatulu m'dzanja langa." Yohane 10: 27, 28.

-ooOoo-

"Kwa Iye amene anatikonda ife, natimasula ku macimo athu ndi mwazi wace." Cibvumbulutso 1: 5b.

2. Okhulupilirayo asanduka wolengedwa watsopano ndi Mzimu wa Mulungu wokhala mwa iye. Tsopano iye afuna kucita cifuniro ca Mulungu.

"Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ali wolengedwa watsopano; zinthu zakale zapita, taonani, zakhala zatsopano." 2 Akorinto 5: 17.

"Tsopano ngati munthu alibe Mzimu wa Kristu, siali wace wa Kristu." Aroma 8: 9b.

3. Wokhulupilirayo, cifukwa cokhala ndi Mzimu wa Mulungu, adzatumikira Mulungu osatumikira Satana.

"Ndi kuti munatembenukira kwa Mulungu posiyana nao mafano, kutumikira Mulungu weni weni wamoyo."
1 Atesalonika 1: 9b.

"Pakuti ife ndife a nchito anzace a Mulungu."
1 Akorinto 3: 9a.

4. Wokhulupilira ali ndi mudzi wosatha m'mwamba ulikumudikira iye.

"M'nyumba ya Atate wanga alimo malo okhalamo ambiri. Ndipo ngati sikudali kotero, ndikadakuuzani inu. Ine ndipita kukakukonzerani inu malo."
Yohane 14: 2.

"Pakuti Ambuye adzatsika Kumwamba mwini yekha ndi mpfuu, ndi mau a mngelo wamkuru, ndi lipenga la Mulungu; ndipo akufa mwa Ambuye adzayamba kuuka: pamenepo ife okhala ndi moyo, otsalafe, tidzakwatulidwa nao pamodzi m'mitambo, kukakomana ndi Ambuye mumlengalenga, ndipo potero tidzakhala ndi Ambuye nthawi zonse." 1 Atesalonika 4: 16, 17.



1. Mulungu anapereka zonse zimene zinali zabwino kwa munthu.

2. Mulungu anakaniza zokha zimene zinali zoipa kwa munthu.

3. Satana, mooneka ngati njoka, anabwera namuyesa Hava. Iye anayesa kumuuza Hava kuti Mulungu anali kumubisira cinthu cina cabwino. Anamuuzitsa Hava kuti Mulungu sakanamulanga ndi imfa ngati akanakhala osamvera.

4. Hava anasankha kukhala osanvera cifuniro ca Mulungu ndipo anadya cipatso coletsedwaco. Ndipo anapereka kwa Adamu nayenso anadyako.

## KUFOTOLOZERA CHIMO

Kucokera pa zinthu tanena pamwambazi, tifuna kudziwa bwino za kuti chimo ndi ciani. Chimo ndilo kukana cifuniro ca Mulungu ndi kuti munthu acite cifuniro ca iye mwini. Ici ndi ceni-ceni cimene adacita Adamu ndi Hava. Adacidziwa cifuniro ca Mulungu koma anasankha kukana cifuniro ca Mulunguco kuti iwo akanakhoza kucita cinthu cimene akanafuna kucita.

## CHIMO LIRI KWA ANTHU ONSE PONSE-PONSE

Mulungu atiphunzitsa ife m'mau ace kuti anthu onse kuli konse anacimwa kwa Iye. Pa maweruzidwe a munthu, tingathe kukhala ngati abwino kwambiri. Koma Mulungu waweruza monga mmene aweruzira munthu. Mulungu atifanizira ife ndi cilungamo cace ca Iye mwini. Pamene Mulungu wacita ici, anena kuti onse anacimwa.

"Pakuti onse anacimwa, naperewera pa ulemerelo wa Mulungu." Aroma 3: 23.

"Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha." Yesaya 53: 6a.

"Tikati kuti tilibe ucimo, tidzinyenga tokha, ndipo mwa ife mulibe coonadi." 1 Yohane 1:8.

"Potero kwa iye amene wodziwa kucita bwino, koma sacita, kwa iye kuli cimo." Yakobo 4:17.

ZOTSATILA ZACE ZA UCIMO

Ncosatheka kulemba mndandanda wa zoipa zonse zimene zabwera pa dziko palansi cifukwa ca ucimo. Mau sangathe kukamba za cisoni ndi zowawa zimene zinabwera ndi cimo. Pamene tiyang'anitsitsa pa dziko lapansi lero ndi zowawa zace, imfa, zonyenga, zidani, nkhondo, cisalungamo, matenda njara, ndi umphawi, tiyenera kukumbukira kuti Mulungu sanalenga dziko lotere. Dziko silinali lotere mpaka nthawi imene chimo linalowa padziko. Makamaka tifuna kulozapo njira ziwiri zimene chimo linaipitsira munthu.

1 <u>Cimo liononga ciyanjano cathu ndi Mulungu.</u>

Pamene chimo linalowa mumtima mwa Adamu ndi Hava, anadziwa kuti anacimwa. Anafuna kubisa umalisece wao ndi kubisalira Mulungu. Cimo lao linawacotsetsa m'munda uja wa Edeni ndiponso pamaso pa Mulungu. Tsopano, monga momwemo, cimo lisiyanitsa ndi Mulungu.

"Koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu, ndipo macimo anu abisa nkhope yace kwa inu, kuti Iye sakumva." Yesaya 59:2.

2. <u>Ucimo ubweretsa cilango cosatha; m'gahena.</u>

"Pakuti mphotho yace ya ucimo ndi imfa." Aroma 6: 23a.

"Ndipo imfa ndi Hade zinaponyedwa m'nyanja ya moto. Iyo ndiyo imfa yaciwiri. Ndipo ngati munthu sanapezedwa wolembedwa m'buku la moyo anaponyedwa m'yanja ya moto." Cibvumbulutso 20: 14,15.

"Koma amantha, ndi osakhulupilira, ndi onyansa, ndi



"Ndi kucitira umboni Ayuda ndi Ahelene wa kutembenuza mtima kulinga kwa Mulungu, ndi cikhulupiliro colinga kwa Ambuye wathu Yesu Kristu."
Macitidwe 20: 21.

CIKHULUPILIRO ndi cikakamizo cimene ciutsa cikhulupiliko pa moyo ku cinthu cimene ucikhulupiliraco. Cikhulupiliro ca Yesu Kristu ndico cikhulupiliro cimene ciutsa munthu kuti moyo wace ukhulupilire pa Yesu. Cipulumutso cilandilidwa pamene cikhulupiliro coteroco caikidwa mwa Iye monga Mpulumutsi ndi Ambuye.

"Pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero, kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupilira Iye asatayike, koma akhale nao moyo wosatha." Yohane 3: 16.

"Ndipo iwo anati, Ukhulupilire Ambuye Yesu, ndipo udzapulumuka, iwe ndi a pabanja ako." Macitidwe 16: 31.

"Popeza tsono tayesedwa wolungama ndi cikhulupiliro, tikhala ndi mtendere ndi Mulungu mwa Ambuye wathu Yesu Kristu." Aroma 5: 1.

"Pakuti muli opulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiliro, ndipo ici cosacokera kwa inu: ciri mphatso ya Mulungu." Aefeso 2: 8.

ZOTSATIRA ZACE ZA CIPULUMUTSO

1. <u>Okhulupilirayo ayeretsedwa ndi kukhululukidwa macimo ace onse.</u>

"Tiyeni, tsono, tiweruzane, ati Yehova; ngakhale zoipa zanu ziri zofiira, zidzayera ngati matalala; ngakhale ziri zofiira ngati kapezi, zidzakhala ngati ubweya wa nkhosa, woti mbu." Yesaya 1: 18.

"Kuti ndidzacitire cifundo zosalungama zao, ndipo zoipa zao sindidzazikumbukanso." Ahebri 8: 12.

2. <u>Njira ya cipulumutso iyi ikhala yotheka kudzera mwa imfa ya Yesu ya pa mtanda yofera ocimwa onse.</u>

"Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya ife tonse." Yesaya 53: 6.

"Monga Mwana wa munthu sanadza kutumikiridwa koma kutumikira ndi kupereka moyo wace dipo la anthu ambiri." Mateyu 20: 28.

"Pakuti ici ndi mwazi wanga wapangano, wothiridwa cifukwa ca anthu ambiri kucotsa macimo."
Mateyu 26: 28.

"Ameneyo sanadziwa ucimo anamyesera ucimo m'malo mwathu; kuti ife tikhale cilungamo ca Mulungu mwa Iye." 1 Akorinto 5: 21.

"Amene anasenza macimo athu mwini yekha m'thupi mwace pa mtanda, kuti ife, titafa ku macimo tikakhale ndi moyo kutsata cilungamo; ameneyo mikwingwirima yace munacilitsidwa nayo."
1 Petro 2: 24.

3. <u>Cipulumutso cilandiridwa pakulapa ndi kukhulupilira.</u>

KULAPA ndiko kusinthika kwa mtima kumene zotsatira zace zionekera pa kusinthika kwa macitidwe a zocita. Kulapa kweni-kweni kukhudza zinthu zitatu; pakudziwa kuti unacimwa kwa Mulungu; pakumva cisoni cifukwa ca ucimo; pakuleka chimo. Mulungu momveka bwino atiphunzitsa ife m'mau ace kuti munthu ayenera kulapa asanalandire cipulumutso.

"Kuyambira pamenepo Yesu anayamba kulalikira, ndi kunena, Tembenukani mitima, pakuti ufumu wa kuwamba wayandikira." Mateyu 4: 17.

"Ndinena kwa inu, Iaitu; koma ngati inu simutembenuka mtima mudzaonongeka nonse momwemo."
Luka 13: 3.



acigololo, ndi olambira mafano, ndi onse amabodza, colandila cao cidzakhala m'nyanja yotentha ndi moto ndi sulfure; ndiyo imfa yaciwiri." Cibvumbulutso 21: 8.

"Pomwepo Iye adzanena kwa iwo a ku dzanja lamanzere, Cokani kwa Ine otembeleredwa inu, ku moto wa nthawi zonse wokorezedwera mdierekezi ndi amithenga ace." Mateyu 25: 41.

Munthu angathe kunyozera kapena kuliseka cimo, koma Mulungu satero. Mulungu aona cimo ndi kulanga cimolo. Tsopano tonsefe tinacimwa ndipo palibe cina cimene tingacite kuti tithawe cilango cimene tiyenera kulandira. Koma Mulungu, m'cikondi cace ca pa ife, anapanga njira yakuti chimo lathu lilangidwe ndipo ife tipulumuke. Phunzirani bwino mutu wa patsogolowu za Cipulumutso.

-ooOoo-

MUTU 6

## CIPULUMUTSO

Pa phunziro lathali tinaphunzira kuti anthu onse ona-cimwa ndipo ali pansi pa ciweruzo ca Mulungu. Pa mutu uwu tifuna kuti tiphunzire za njira ya cipulumutso imene Mulungu anapereka mwaulere kwa anthu onse kudzera mwa Mwana wace, Yesu Kristu. Cinthu coyamba cimene tiyenera kuzindikira ndi ici:

### MUNTHU SANGATHE KUDZIPULUMUTSA YEKHA

Tiyeni tiganizire zifukwa zinai za kuti munthu sangathe kudzipulumutsa yekha:

1. Munthu sangathe kudzipulumutsa yekha cifukwa cilungamo ceni-ceni cimene iye angathe kuonetsa cili coperewera kutali ndi cilungamo cimene cili cokondweretsa pamaso pa Mulungu.

   "Pakuti tonse takhala ngati cinthu cosakonzeka, ndi zolungama zathu zonse zili ngati cobvala codetsedwa." Yesaya 64: 6a.

2. Munthu sangathe kudzipulumutsa yekha cifukwa Mulungu atiuziratu kuti palibe munthu adzapulumuka cifukwa ca nchito zace.

   "Pakuti muli wopulumutsidwa ndi cisomo cakucita mwa cikhulupiliro, ndipo ici cosacokera kwa inu; ciri mphatso ya Mulungu; cosacokera ku nchito, kuti asadzitamandire munthu ali yense." Aefeso 2:8, 9.

3. Munthu sangathe kudzipulumutsa yekha cifukwa ayenera kulandira mphotho ya macimo ace ----imfa.

   "Pakuti mphotho yace ya ucimo ndi imfa."
   Aroma 6: 23a.



4. Munthu sangadzipulumutse yekha cifukwa munthu wocimwa ali wakufa kale mu uzimu. Tiwelenga Buku Lopatulika kuti munthu asanalandire moyo watsopano kudzera mwa Yesu Kristu, ali wakufa m'zolakwa ndi macimo.

   "Ndipo inu, anakupatsani moyo, pokhala munali akufa ndi zolakwa, ndi zocimwa zanu." Aefeso 2: 1.

   Monga momwe amakhalira munthu wakufa m'moyo wathupi kuti sangathe kucita kanthu, momwemonso, munthu wakufa mwauzimu sangathe kucita kanthu kakudzipatsa yekha moyo wauzimu.

### MULUNGU ANAPEREKA NJIRA YA CIPULUMUTSO CA MUNTHU

1. Njira ya cipulumutso iyi ndiye Yesu.

   Pali anthu ambiri amene amadziwa kuti sangathe kudzipulumutsa okha ndi kuti ayenera kupeza thandizo. Komatu amalakwa pakuyang'ana kucinthu cacabe kuti apeze thandizo. Ena akhulupilira mu ubatizo wao. Ena akhulupilira pakukhala ciwaro cimodzi ca mumpingo wao. Ena akhulupilira mu mneneri wonama. Alipo ena amene amakhulupilira mu ufiti ndi m'mafano. Mulungu anapereka njira imodzi ya cipulumutso ya kwa anthu onse a pa dziko lapansi ndipo njira iyi ili mwa Yesu Kristu. Yesu ndipo Yesu yekhayo angathe kutipulumutsa ife ku macimo athu ndi kucilango cosatha ca ku gahena.

   "Yesu ananena naye, Ine ndine njira, ndi coonadi, ndi moyo: Palibe munthu adza kwa Atate, koma mwa Ine." Yohane 14: 6.

   "Ndipo palibe cipulumutso mwa wina yense, pakuti palibe dzina lina pansi pa thambo la kumwamba, lopatsidwa mwa anthu, limene tiyenera kupulumutsidwa nalo." Macitidwe 4: 12.